


KHRISTU AKUWULULIDWA

MU MAWU AKE OMWE

 Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu. Ambuye Yesu, M’busa wa Nkhosa zambiri, ife tiri angongole kwambiri kwa Inu, Ambuye, kuti ife sitingakhoze konse kukulipirani Inu chifukwa cha chikondi chimene Inu mwachikhetsera mochuluka mu mitima yathu. Ife tikumverera osayenera kwambiri pamene ife taweramitsa mitu yathu ndi kuima mu kukhalapo Kwanu. Ife tikukupemphani Inu kuti mutiyeretse ife ku zolakwitsa zonse ndi tchimo lonse. Ife tikupemphera kuti Inu mulimbikitse matupi athu lero. Ambiri ali odwala ndi osautsika, monga izo zikusonyezedwa pano, pa mipango ndi zopempha zikubwera muno pa lamya ndi kulikonse.

² Ndipo ife tikukhulupirira kuti ife tiri kutsirizitsa mbiriyakale ya dziko lino tsopano, ndipo posakhalitsa nthawi izimirira mu Umuyaya, ndipo ife tikufuna kuti tikhale okonzekera kwa ora limenelo. Ndicho chifukwa ife tasonkhana pano mmawa uno, ndi kuti tidzakonzekere nthawi imeneyo. Ine ndauzidwa kuti alipo ochuluka ali pa kulumikiza kwa lamya mmawa uno ku fuko lonse, kuchokera ku gombe mpaka ku gombe. Kulikonse kumene mawu athu akufikako, mulole gulu laling’ono ilo lidalitsidwe. Muchiritse odwala amene ali pakati pawo, ndipo ine ndikupemphera kuti Inu muyeretse miyoyo yawo ku zoyipa zonse. Ndipo mutithandize ife pano mmawa uno, pa kachisi, kuti nafenso tikhoze kusangalala nawo mwayi wawukulu umenewo.

³ Ndipo ife tikupempha kuti Inu muyankhule kwa ife lero kupyolera mu Mawu Anu olembedwa, ndipo mulole Mzimu uwulule kwa ife zinthu zimene ife tiri kuzisowa, pamene ife tasonkhana kwa fuko lonse tsopano, tikumverera kuti ife tiri anthu aang’ono, koma tiri nawo malo pakati pa owomboledwa, chifukwa ife takhulupirira pa Yesu Khristu. Perekani zinthu izi kwa ife, Ambuye.

⁴ Ndipo pamene ife tizitseka msonkhano ndipo ife tikamapita ku makwathu kosiya mu fuko lonseli, mulole ife tikanene, monga aja aku Emau, “Kodi mitima yathu sinatenthe mkati mwathu pamene Iye amayankhula kwa ife mu njira yonse?”

⁵ Tsopano, Atate, ine ndikudziwa kuti chirichonse chimene ine ndingati ndinene chikanati chikhale ndithudi chosakwanira, ndi—Akhristu abwino mu fuko lonseli tsopano amene atchera kuno, izo sizikanati zikhale—izo sizikanati zikhale zokwanira. Izo sizikanati zikhale chinachake chimene ine ndikanati ndinene

chimene chikanakhoza kuchita ubwino uliwonse, chifukwa ife tonse tiri mu gulu lomwelo. Ndife anthu, achivundi. Koma mulole Mzimu Woyera waukulu uyankhule; mumulole Iye awagwire Mawu ndipo angodziwulula Yekha. Ife tiri kuyembekezera pa Iye tsopano, mu Dzina la Yesu. Amen.

Inu mukhoza kukhala.

⁶ Ine ndinakhala ngati...kudzidabwa ndekha. Ine ndinamuza mkazi wanga, ngati iye apezeka akumvetsera kuno, ku Tucson uko, kuti ine sindimaganiza kuti ine ndikanakhala ndi msonkhano uliwonse pamene ine ndimabwerera; ndipo ine sindinabweretse nkomwe zovala. Ndipo ine ndinanena kwa mpongozi wanga wamkazi, iye anali atasita jekete yanga, ndipo ine ndinati, “Ine ndikuyima kuseri kwa guwa, ndi... Iwo sakudziwa kuti tharauza ndi ya mtundu wina ndi jekete winawake.” Ndizo zimene ine ndimavala kunyumba. Koma, Meda, iye anasita malaya anga ndi chirichonse, chotero zonse... Usati udandaule; chirichonse chiri bwino.

⁷ Tsopano, ife tiri ndi chopempha pano, kuti pali m’bale wokondedwa kwambiri...Ndipo ine ndikuganiza kuti—kuti Prescott, ine ndikukhulupirira, alumikizidwa kuno mmawa uno, uko mu—mu Prescott, Arizona. Bambo ake a Mlongo Mercier anali basi ali pa njira yao wa kuno ku msonkhano, ine ndamva, ndipo achita kuwatengera ku chipatala ndi vuto la mtima, M’bale Coggins. Ndipo, nayenso, M’bale Junior Jackson, ine ndikuganiza iye ali pa walesi inayo uko, kapena lamy inayo uko mu Clarksville kapena New Albany, ndipo bambo ake ali mu chipatala, ine ndamva, ali ndi opareshoni yowopsya ya khansara mu chiwindi. Chotero ife tikufuna ndithudi kuwakumbukira amenewo mu mapemphero athu. Ndipo tsopano alipo ena pano, nawonso, koma ife sitikufuna kuti titenge nthawi. Mulungu akudziwa zonse za iwo, chotero tiyeni ife tiwapempherere iwo tsopano.

⁸ Wokondedwa Mulungu, pamene wokondedwa uyo, wachikulire, bambo wa dzanja lamakwinya, M’bale Coggins, wankhondo wakale wa mmundawu, ali...kugona mu chipatala mmawa uno, kwinakwake, akuvutika ndi vuto pa mtima wake. Mulungu, mtima wokalamba wosawuka uwo wadutsa mu mavuto ochuluka. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mumuthandize iye. Perekani izi. Iye monga...Iye amaukonda moyo monga tonse ife timachitira, ndipo iye akufuna kuti akhale moyo. Ambuye Mulungu, perekani izi. Ife mu fuko lonseli tikupemphera mu Dzina la Yesu chifukwa cha iye, kuti Inu mumuchiritse iye ndi kumulutsako iye. Ife tikukhulupirira kuti Inu mutero; iye abwera kumene ku msonkhanowu.

⁹ Ife tikumupempherera M’bale Jackson, bambo ake ofunika amene agona uko pafupi imfa tsopano, ndipo anabweretsa mu dziko mnyamata wabwino monga Junior. Ine—ine—ine

ndikupemphera, Mulungu wokonedwa, kuti Inu mumuchize iye. Ine ndikudziwa kuti izo zikuwoneka zosatheka. Mankhwala, madokotala, iwo—iwo sakudziwa choti achite mu vuto la mtundu umenewo. Koma ife tikukumbukira M'bale Hall, nayenso, pamene asing'anga opambana kwambiri kuno ananena, mu Louisville, anati, "Iye wangotsala maora pang'ono kuti akhale moyo," ali ndi khansara mu chiwindi. Ndipo iye ali moyo lero, ndipo izo ndi zaka makumi awiri ndi zisanu zapitazo, chifukwa cha chisomo Chanu. Chotero ine ndikupemphera kuti Inu muwachiritse M'bale Jackson lero, Ambuye, mulole chisomo Chanu ndi chifundo zikhale ndi iye.

¹⁰ Ndipo mulu wonse uwu wa mipango ndi zovala ndi zinthu zimene zayikidwa pano mwa kupempha; Inu mukuwadziwa iwo onse, Atate. Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke machiritso kwa iwo onse. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

¹¹ Tsopano kuyamba, mmawa uno, ine sindinali kuganiza kuti ine ndikanati ndibwere kuno, pa malo oyamba, Lamlungu latha. Ndiyeno kachiwiri, pamene ife tinalengeza izo, ine ndinabwera kuno. M'bale Neville anati ine ndiyankhule! Ndiyeno ife tinalengeza kuti tidzakhale kuno lero, ndipo izo sizinawuzidwe kunja kuzungulira dziko kwa anthu. Ndipo ife tiri ndi dongosolo la lanya ili tsopano, limene liri kwambiri, labwino kwambiri. Anthu akhoza kukhala mu manyumba awo momwe kapena awo. . . kusonkhana mu malo awo, mipingo yawo, ndi zina zotero, ndi kumamvetsera ulaliki. Ine ndikuyamikira izo.

¹² Tsopano ine ndikuwona zitaikidwa pano, pakhala pali zopempha zochuluka sabata latha ili, pa chimene ine ndinanena Lamlungu latha pa Uthenga. Ine ndikukhulupirira ine ndaiwala chimene ine ndinawutcha iwo tsopano. Koma ine ndinanena chinachake za kupereka ngongole zanu. Ndipo inu mukudziwa, ziribe kanthu chimene iwe unena, izo sizimamvetsedwa ndi ochuluka. Osati chifukwa iwo. . . iwo samafuna kuti asamvetse izo, koma inu basi mophweka simumazimvetisa izo.

Ndipo tsopano wina anati, "Kodi ife tizigula galimoto?" Kapena, "Ine ndiyenera kutani. . ."

Tsopano, izo sindizo zimene Yesu ananena, kapena Baibulo pamenepo, zimene linati, "Musakhale ndi ngongole kwa munthu." Ndi ngongole zokhalitsa zimene inu mukanakhoza kuzilipira. Lipirani izo. Izo sindizo. . . Ndiko kusakhala ndi ngongole kwa munthu. Izo sizikutanthauza. . . Mai, ife tiri ndi ngongole ya rendi, ngongole yathu ya lanya, ife. . . ndi kaya zina chiani. Ife—ife tiri ndi ngongole ya zinthu zimenezo, ndipo ife timalipira izo. Koma, ngongole yakale yokhalitsa imene inu mukanakhoza kulipira, lipirani iyo yonse. Mukuona? Tsopano, musati muzipita ndi chirichonse chikulendewera pa inu monga choncho.

¹³ Ine ndikukumbukira nthawi imene ine ndinali kudwala, nthawi yina pamene ine ndinali mnyamata. Ine ndinatuluka ku chipatala ndiri ndi ngongole ya pafupi madola zikwi ziwiri. Ndipo kunali sitolo ya mankhwala kuno, Bambo Swaniger, ine ndinali nawo iwo ngongole ya pafupi madola mazana atatu kapena anai, ndalama za mankhwala. Iye sanali kundidziwa nkomwe ine. Ndipo bamboyo...ine ndinapita kwa iye. Ine sindinali kumudziwa iye. Ndipo iye anangowatumiza iwo uko, mulimonse, sanakane konse kuti awatumize iwo. Ndipo ine ndinati, "Ine ndiri nanu ngongole." Ndipo ine ndinati...ine ndikukhulupirira, Swaniger...Iwo anali Bambo Mason uko ku Kanjira ka Court ndi Spring.

Ndipo ine ndinati, "Ine ndiri nanu ngongole inu. Ndipo ine—ine ndikadali wofooka moyipabe, koma ine ndikuyesera kumapita ku ntchito. Tsopano, ngati ine sindingakhoze kukulipirani inu... ." Ine ndinali nditakhala kumene Mkhristu. Ine ndinati, "Chinthu choyamba, Bambo Mason, monga ntchito yanga kwa Mulungu, ine ndiri Naye ngongole ya zakhumi zanga. Ine ndikufuna kuti ndizilipira kwa Iye zakhumi zanga, poyamba." Ndipo ine ndinati, "Ndiye ntchito yanga yotsatira ndi kulipira ngongole zanga." Ine ndinati, "Bambo anga ndi odwalika, ndipo iwo... Ndipo ife tiri nawo... Tiripo khumi a ife ana mu banja." Koma ine ndinati, "Ine nditi... Ngati ine sindingakhoze kukulipirani inu moposa masenti makumi awiri ndi asanu pa ngongole imeneyo, pa tsiku lamalipiro lirilonse; ngati ine sindingakhoze kukulipirani inu ngakhale masenti makumi awiri ndi asanu, ine ndizibwera ndi kudzakuuzani inu za izo. Ine ndizikuuzani inu, 'Ine—ine—ine sindingakhoze kuchita izo nthawi ino.'" Tsopano, mwa kuthandizidwa ndi Mulungu, ine ndinalipira pang'ono paliponse. Mukuona? Koma ndicho chimene ine ndikutanthauza, mukuona? Wina asamangonena kuti...

¹⁴ O, Mkhristu wina pano pa mpingo nthawi ina anapita kwina ndipo anakagwira ntchito ina pa galimoto kuno, ndipo bamboyo anabwera kuno... Bamboyo anati, "Ine ndikulipirani inu. Ine ndimalipidwa Loweruka," kapena chinachake chimzake. Ndipo iye sanamulipire konse iye. Ndipo masabata pambuyo pa masabata anadutsa, ndipo sanamulipire konse iye, sananene nkomwe mawu. Ndipo—ndipo munthuyo anabwera ndipo anadzandifunsa ine, iye anati... Mwaona, izo zimawonekera motsutsa mpingo. Izo zimawonekera motsutsa Khristu.

Inu mukalephera kumulipira iye, muzipita kukamuuza iye, kuti, "Ine ndiri nanu ngongole, ndipo ine ndidzakulipirani inu. Ine ndine Mkhristu, koma ine—ine basi... ine sindingakhoze kuchita izo pakali pano, ine ndiyenera... ine ndiri ndi ngongole imeneyi." Ndipo, kumbukirani, izo ziri pa mabuku a Mulungu naponso, inu mukudziwa, zimene inu muchita. Chotero ndizo...

Ine ndikuyesera kutero, kwa inemwini ndi kwa tonse ife limodzi, kuyesera kuti tikhale okonzeka, pakuti ife tikudziwa kuti tiri kuyandikira chinachake, tayandikira kwambiri chinachake chimene chiti chichitike. Chotero ife tikufuna kuti tikhale okonzeka. Pamene Kudza kwa Ambuye kuli kuyandikira pafupi kwambiri tsopano, ife tikufuna kuti tikhale okonzekera ora lalikulu ilo.

¹⁵ Tsopano ife tikufuna kuti tikhale okonzekera ndi kuyankhula tsopano pa phunziro laling'ono pano limene ine ndinalisankhira mmawa uno, mwa kuthandiza kwa Ambuye. Ndipo ife tiyankhula mwachidule basi monga ife tingathere, chifukwa cha kulumikiza kwa anthu. Ine ndikuyembekeza inu nonse muli...konse mu fukoli, muli ndi mmawa wabwino monga ife tiri nawo kuno mu Indiana. Kwabwino, kozizira, nyengo yabwino ife tiri nayo kuno tsopano chiyambireni mvula. Ndipo ndi kwabwino kwambiri.

¹⁶ Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 1; ndi kuchokera ku Bukhu la Yohane Woyera, mutu wa 1. Ahebri 1:1 mpaka 3, ndi Yohane Woyera 1:1, kwa nkhaniyo. Phunziro langa mmawa uno liri kuphunzira mu Malemba. Tsopano tiyeni tiwerenge Ahebri 1:1.

Mulungu, yemwe mu nthawi zakale...mkachitidwe kosiyana ankayankhula mu nthawi zakale kwa makolo athu mwa aneneri,

Koma mu masiku otsiriza ano wayankhula kwa ife mwa Mwana wake, yemwe iye wamukhazika wolowa wa zinthu zonse, kupyolera mwa iyenso iye analenga dziko;

Amene pokhala ali mwa kuwala kwa ulemerero wake, ndi...chifaniziro chofotokozedwa cha umunthu wake, ndipo akugwirizira zinthu zonse ndi mawu a mphamvu yake, pamene iye anali mwa yekha atayeretsa machimo athu, anakhala pansu pa dzanja lamanja la Ukulu mmwambamo;

Ndi zowerenga zokongola bwanji! Tsopano Yohane Woyera 1:1.

Pa chiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.

¹⁷ Tsopano, ndipo nkhani yanga mmawa uno ndiyo: *Khristu Akuwululidwa Mu Mawu Ake Omwe*. Tsopano, pamene ine ndinafikira pa kugamula kuti ndiyankhule pa izi, zinali chifukwa kuti...Podziwa kuti zimene ife tinena ife tisati tizingonena chifukwa ife tasonkhana limodzi kuti basi mwachisawawa tiziyankhula pa chirichonse, koma ndi chinachake chimene chiti chithandize kuwakhazikitsa anthu, pakuti ife tikuti tidutse mu madzi owopsya, angozi. Ife

tikusambira kale kupyola mu iwo. Ndipo nthawizina ine ndikulingalira kuti izo ziri ndi inu monga izo ziriri ndi ine, kuti zimawoneka monga chomwecho, zochuluka kwambiri za izo, ndi zowopyeza chotero.

¹⁸ Ine ndinali kungoyankhula kwa mtumiki wamng’ono ndi mkazi wake, mu chipinda, mphindi pang’ono chabe zapitazo. Ndipo onse a iwo ali amanjenje mofanana basi ndi dziko lonse, anthu ena onse a dziko lapansi. Ine ndinati, “Kumbukirani, Satana ali nayo nk’honya imene ikubwera pa inu.” Palibe kusamala yemwe inu muli, Mulungu. . .Iye ali nawo ufulu wa nk’honya imodzi imeneyo. Inu mukanafuna mwina kuti nk’honya imeneyo, ikhale chiani; ikhale khungu, kapena ikhale nyamakazi mutakhala mu mpando, kapena ikhale manjenje? Mukuona? Iye ali napo penapake pamene iye akhoza kukumenyani inu. Iye ali nawo ufulu wa pa malo otseguka amenewo. Tsopano, ndiwo malo amene inu muyenera kuti muziwaphimba nthawi zonse. Ndipo powona m’badwo wamanjenje uno umene ife tiri kukhalamo!

¹⁹ Ndipo matepi a sabata yatha, ine ndikuganiza, awulula kwa inu zinthu zazikulu zowopsya zimene ife tikuti tiyankhulepo limodzi la masiku amenewa pamene ife titi tipeze malo okwanira, pa kutseguka kwa miliri yotsiriza iyo imene iti itsanuliridwe pa dziko lapansi, Mbale zimenezu, kani, kutsanulira kwa Mbale, ndi Mabingu Asanu ndi awiri, ndi zowoneka mowopsya izo zimene zikubwera pa dziko lapansi. Munthu tsopano, ndipo anthu lero, ali mu chikhalidwe chamanjenje choterocho; dziko lonse!

²⁰ Inu mukawerenge *Reader’s Digest* ya mwezi watha uwu, inu mukazindikira phunziro mmenemo; ziri pa Billy Graham, mlaliki wamkulu. Iye anafika potopa kwambiri iye sakanakhoza basi kuti achititse misonkhano yake, ndipo iye—iye anapita ku chipatala cha a Mayo kuti akapimidwe mthupi. Palibe kanthu kovuta ndi iye, kupatula kuti iye samachita ntchito yokwanira basi. Ndipo iwo amuka iye kuti azithamanga; kulimbitsa thupi. Iye akumathamanga mailo tsiku lirilonse.

Ndiyeno nk’haniyo ikupitirira kunena kuti sayansi yatsimikizira kuti lero, kuti ana aang’ono, anyamata aang’ono awa ndi asungwana, “akugunda usinkhu wawo wapakati pa usinkhu wa zaka makumi awiri.” Ndipo akamafika makumi awiri ndi zisanu, nthawi zambiri, mwa ochuluka, asungwana akumakhala atadutsa kusintha kwa thupi, pa usinkhu wa zaka makumi awiri ndi zisanu.

Ine sindikudziwa ngati inu mumadziwa izo kapena ayi, koma usiku pang’ono wapitawo pamene Mzimu Woyera unali ukuyankhula muno mu msonkhano, msungwana wamng’ono atakhala pansu muno, ndicho kwenikweni chimene chinali chovuta ndi mwana ameneyo pamene iwo unamayitana. Ine ndinayang’ana pa iye nthawi yachiwiri, ndinayang’ana

kachiwiri, ndipo ine ndinawona limene linali vuto. Ine ndiganiza, “Izo sizingakhoze kukhala; mwana ameneyo ndi wamng’ono kwambiri.” Koma iko kunali kusintha kwa thupi, pafupi usinkhu wa zaka makumi awiri, makumi awiri ndi zitatu, chinachake monga choncho. Mukuona?

²¹ Mayi anga ndi amayi anu anagunda usinkhu umenewo ali pafupi makumi anai ndi zisanu mpaka makumi asanu. Mkazi wanga anagunda usinkhu umenewo ali pafupi makumi atatu ndi zisanu. Tsopano izo zatsika mpaka makumi awiri. Mtundu wonse wa anthu wavunda. Chabwino, ngati umunthu uwo wa thupi lathu uli kuphwasuka monga chomwecho chifukwa chakudya zakudya za haibridi, kumangika, izo zalivunditsa ilo, kodi ichonso sichiri kuvunditsa makhungu aubongo? Ndiye ife tikukhoza kuwona momwe akazi akhoza kupita pa msewu, amaliseche. Ife tikukhoza kuwona momwe iwo akhoza kuthamangira kudutsa—mmisewu pa mailosi zana ndi makumi awiri pa ora, zinthu zonse izi. Izo zafika pamalo pamene fuko lonse, dziko lonse, osati kokha fuko lino, koma kulikonse, mwamalingaliro lapita.

²² Ndiyeno pamene ife titsegula izo, Ambuye akalola, pa Mbale Zisanu ndi ziwiri izo ndi kusonyeza zinthu zowopsya izo. Anthu adzakhala amisala kwambiri, pakapita kanthawi, mpaka iwo azidzalingalira kuti akuwona nyerere za usinkhu wa phiri. Izo zidzakhala zikuwazunza akazi; padzakhala dzombe liti lidzabwere pa dziko lapansi, liri ndi tsitsi lalitali, kuti liziwazunza akazi amene amadulamo lawo; tsitsi ngati akazi, likulendewera pansu; ndi mano aatali, ngati mkango; mbola ku nchira kwake, ngati nankalizi, ndi—ndi zina zotero, kuti ziziwazunza anthu pa dziko lapansi. Komano apo zidzakhala ziri mochedwa kwambiri kuti achite chirichonse nazo. Inu mukonzeke pakali pano. Kuzunza!

²³ Ndipo Lamlungu lapita pamene ife tinali kupita mu mikombelo ija, ya momwe zokhudzira zisanu pa gawo lakunja. Ndizo mipita, zokhudzira zisanu kwa thupi. Pali njira imodzi yokha imene inu mungafikire ku thupi, ndiyo mwa zokhudzira zisanu zimenezo: kuwona, kulawa, kumverera, kununkhiza, ndi kumva. Palibe njira ina imene inu mungalikhudzire—thupi.

²⁴ Mkati mwa munthu ameneyo muli munthu wotchedwa mzimu, ndipo iye ali nazo zokhudzira zisanu: kuganiza, ganizo. . . ndi ganizo, ndi kukonda, ndi chikumbumtima, ndi zina zotero. Chabwino.

²⁵ Tsopano, iwe sungakhoze kuganiza ndi thupi lako. Iwe umaganiza ndi malingaliro ako. Ndipo mmenemo ndi momwe ochuluka kwambiri, a Akhristu, amangoyimira. Ndipo iwo akhoza, monga ngati chimanga mmunda ndi maudzu mmunda, iwo akhoza kudzozedwa ndi Mzimu Woyera womwewo umene okhulupirira enieni amadzozedwa nawo.

Koma pansi mkati mwake, gawo lotsatiralo, gawo lachitatu, ndilo solo; ndipo iyo ndi yokonzedweratu ndi Mulungu. Umo ndi momwe nyongolosi yeniyeni ya mbewu imakhala, ndi mkati mmenemo.

²⁶ Ndipo, kumbukirani, ngati ine nditatenga chisoso ndi kuchidula icho motsegula, kumezanitsa mkati mwa icho mtima wa—wa tirigu ndi kuwuyika iwo mmenemo, kumukwirira iye, iye akanati adzabale tirigu kuchokera mu chisoso; ziribe kanthu chimene kunjako kuli, zotengeka zake.

²⁷ Lero, asokonezedwa nazo kwambiri za umboni wa Mzimu Woyera, ndi zina zotero. Satana akhoza kusanzira mtundu uliwonse wa mphatso imene Mulungu ali nayo, koma iye sangakhoze kuwabweretsa Mawu amenewo, Mawu ndi Mawu. Ndi pamene iye analephera mmunda wa Edeni. Ndi pamene iye nthawizonse amalepherera. Ndi pamene iwo, tepi pa mwabodza “iwo odzozedwawo, abodza,” kapena iwo odzozedwawo; iwo akhoza kudzozedwa ndi Mzimu, kumayankhula mu malirime, kuvina, kufuula, kulalikira Uthenga, ndipo nkukhalabe ali mdierekezi.

Ndi chamkaticho! Tsopano kumbukirani, Yesu anati, “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine. Palibe munthu angabwere kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.”

Tsopano, ife tinazitenga kudutsa phunziro, kuti tisonyeze kuti mkati. . . Inu munali mwa agogo-agogo-agogo-agogo anu aamuna, njira yonse mmbuyo, kuyankhula mwathupi. Ndiye, ndicho chimene inu muli mwa umunthu wanu, chibadwa. Nthawizina mwana akhoza kubadwa m’banja, wamutu-wofiira. Izo zimawadabwitsa bambo, chifukwa palibe aliyense yemwe iye akumudziwa, wa makolo ake, wamutu-wofiira, kapena kwa amai. Koma ngati inu mutati mupite kutali mmbuyo ku mibadwo ingapo, inu mukapeza kuti wina anali wamutu-wofiira. Mbewu imeneyo imakhala ikubwerabe pansi, ndipo inu mumadzakhala chibadwa cha wina wochokera kutali mmbuyo.

Zofanana monga Ahebri mutu wa 7 amanena, kuti, “Melkizedeki, Abrahamu anapereka zakhumi kwa Iye pamene iye anali kubwerera kokapha mafumu. Ndipo Levi, yemwe ankalandira zakhumi, anapereka zakhumi,” pakuti iye anali mu chiuno cha Melkizedeki ku. . . kapena, “chiuno cha Abrahamu,” kani, pamene iye anakomana ndi Melkizedeki.

²⁸ Tsopano chinthu chomwecho ndi ichi. Ngati iwe uli mwana wamwamuna wa Mulungu, ndipo ngati ine ndiri mwana wamwamuna wa Mulungu, kapena mwana wamkazi wa Mulungu, ife tinali mwa Mulungu pachiyambi. Ndipo pamene Yesu anadzakhala chidzalo cha Mawu, ndiye ife tinali mwa Iye, mmawonekedwe a nyongolosi. Pamene Iye anali kupachikidwa, ife tinapachikidwa mu thupi Lake. Pamene Iye anawuka kwa akufa, ife tinawuka ndi Iye. Ndipo tsopano, pakuti ife

tazindikira izo, “tsopano ife tikukhala limodzi ndi Iye, mu malo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu.” Mukuona? Pakuti Iye. . . Ife, ngati ife tiri ana aamuna ndi ana aakazi a Mulungu, ndife ana a Mulungu, ndiye ndife zokhumba za Mulungu. Ndiye ife tinali. . . tiri nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo Mulungu ndi Moyo Wamuyaya wokha umene ulipo. Ndiye, ife tinali mwa Iye kuchokera pachiyambi. Ndipo pamene Yesu anadzakhala Mawu onse awo, ndiye ife tinali gawo la Iye pamene. Ameni! Ndi inu pamene. Pamene izo ziri mmenemo, palibe mdierekezi, palibe mphamvu, palibe kanthu kalikonse kangakhoze konse kusuntha izo. Ndicho chikhomo chomangirizapo cha solo.

²⁹ Iwe ukhoza kukhala wodzozedwa kunja *kuno*, mu mzimu uwu, ndipo nkumakhumba, ndi kumachita zinthu zina zonse izi. Koma pamene izo zifika pa chikhomo chomangirizapo ichi kwa Mawu awo, iwe sungasunthe konse kuchokera pamene. Icho chimagwira mokhazikika ndi moona, kwa Mawu amenewo, monga izo zingakhoze kukhalira. Kunja kwa icho, mosasamala chimene iwe uchita, iwe ukanali wotayika.

³⁰ M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya uwo, “wamaliseche, wakhungu, womvetsa chisoni; osamadziwa nkomwe izo.” Mukuona, ndi kunjako. . . Ndi odzozedwa awo, odzozedwa ndi Mzimu weniweni. Mukuona, Mzimu Woyera umenewo ukhoza kugwera pa munthu, mu mzimu wake. Koma solo yake ndiyo nyongolosi yake; nyongolosi imeneyo ndi Mawu. Mukuona? Ndipo motani. . . Ine sindikusamala kuti mumalalikira mochulukira bwanji, mumachita *izi* mwabwino bwanji, ndi kuchulukira kwa momwe inu mumakondera; ndi chimodzi cha mipita yaku mzimu. Inu simungakhoze kukonda ndi thupi lanu; inu mumakonda ndi mzimu wanu. Ndi umodzi wa mipita. Ndipo iwe ukhoza kukonda, ndipo ngakhale kumamukonda Mulungu, ndipo nkusakhale wolondola. Iwe ukhoza kutulutsa ziwanda, ndi kulalikira, ndi kuchita zinthu izi; komabe nkusakhala wolondola. Yesu ananena chomwecho, anati ambiri adzabwera mu tsiku limenelo. Mawu awo amakhazikitsa izo!

Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.

Ndipo Mawu anasandulika thupi, ndipo anakhala pakati pathu, . . .

³¹ Zindikirani, ine ndikuti ndiyankhule pa phunziro ili la Baibulo, la, *Khristu Kuwululidwa Mu Mawu Ake Omwe*. Pamene ine ndinatengerapo kugamula uku, munali mu chipinda changa.

Munthu wina wokondeka, mwina wakhala pano mmawa uno. . . ine ndiri nacho chithunzi chitapachikidwa mowerengera mwanga kumtunda uko, ndicho chithunzi cha Hofmann cha *Mutu wa Khristu*, chitalembedwa mu Madalitso. Ndipo mpaka pamene iwe umafika pa malo ngati kuti iwe umasowa gawo

la tsitsi, iwo anakanikiza zolimba pang'ono pa cholemba pamene iwe ukudutsa gawo limenelo. Apo, ndi Uyo pamene, atakhala mu Mawu Ake, akuyang'ana kunja komwe; Khristu mu Madalitso. Winawake, aliyense yemwe iye anali, ine ndikukuthokozani inu chifukwa cha icho.

Ndipo wina anabweretsa chithunzi chimenecho ndipo anadzachiyika icho mowerengera mwanga uko, cha Eliya akupita kumwamba mu galeta wa moto. Ife tikuyamikira zinthu zimenezi. Nthawi zambiri, unyinjira ukakula, ine sindimapeza basi mpata woti ndiyankhule ndi kunena zinthu izi, koma ine ndimaziwona izo, m'bale, mlongo. Ine—ine ndikuzidziwa izo, ndipo Mulungu akuzidziwa izo.

³² Tsopano ine ndikuti ndiyankhule pa phunziro ili la: *Khristu Kuwululidwa Mu Mawu Ake Omwe*. Momwe, mu Madalitso, apo payima chithunzi cha Khristu, atayima apo pomwe, monga. Ndi pamene ine ndinalingalira za phunziro ili. Tsopano, Khristu ndi Mawu ali ofanana. Mukuona?

³³ Iwo amati, “Baibulo linali motani . . .?” Anthu amanena. Ine ndinali nditakwera ndi munthu osati kale litali. Iye anati, “Taganizani za izo. Ife pano pa dziko lapansi lino, momwe ife tiriri, ndipo ife timadziwa kokha kapena timangokhoza kunena kuti ife tinapulumsidwa ndi nthano ina ya Chiyuda yotchedwa Baibulo.”

³⁴ Ine ndinati, “Bwana, ine sindikudziwa momwe inu mukunenera izo, koma ine sindiri kukhulupirira kuti ndi nthano ya Chiyuda,” ine ndinatero.

Iye anati, “Chabwino, inu mukamapemphera, kodi inu mumapemphera kwa ndani? Ine ndinapempha *zakuti-ndi-zakuti* ndi zinthu zina; ine sindinazilandire izo.”

³⁵ Ine ndinati, “Inu mumapemphera molakwika. Ife tisamapemphere konse kuti tisinthe malingaliro a Mulungu; ife tiyenera kumapemphera kuti asinthe malingaliro athu. Malingaliro a Mulungu samasowa kusinthidwa kulikonse. Mukuona? Taonani, ndiko kulondola.” Ine ndinati, “Osati zimene inu munalikuzipempha . . .”

Ine ndikumudziwa mnyamata wamng'ono wa Chikatolika, nthawi ina, anali ndi bukhu la pemphero, akunena mapemphero, ndi kuti amayi ake akhale moyo. Ndipo iwo anafa, ndipo iye anaponyera bukhu la pemphero mu moto. Chabwino, taonani, ine sindimayendera bukhu la pemphero; koma, mulimonse, mwaona, inu mumatenga cholinga cholakwika. Inu mukuyesera kuti muzimuwuzwa Mulungu choti achite.

Pemphero liyenera kukhala, “Ambuye, ndisintheni ine kuti ndiziyenera Mawu Anu.” Osati, “Sinthani,” osati, “ndiroleni ine ndisinthe malingaliro Anu. Inu musinthe malingaliro anga.” Mukuona? “Inu musinthe malingaliro anga kwa

chifuniro Chanu. Ndipo chifuniro Chanu chinalembedwa muno mu Bukhu. Ndipo, Ambuye, musati—musati munirole ine kuti ndipite mpaka Inu mutatenga anga—malingaliro anga atakhazikidwa basi monga malingaliro Anu. Ndiyeno pamene malingaliro anga akakhazikidwa monga malingaliro Anu, ndiye ine ndikhulupirira Mawu aliwonse amene Inu munawalemba. Ndipo Inu munati, mkati umo, Inu mudzapanga ‘chirichonse kugwirira ntchito limodzi kwa ubwino’ wa iwo amene amakukondani Inu. Ndipo ine ndimakukondani Inu, Ambuye. Izo zonse zikugwirira ntchito limodzi kwa ubwino.”

³⁶ Ine ndakhala ndiri sabata ino uko kumudzi, ndimakhala ndi abwenzi ena okonededwa kwambiri. Ine ndinawafunsa ena a iwo pa gome, dzulo, pamene ife tinali kudya. Ife nthawizonse timakhala mozungulira ndi kukhala pang’ono. . . ngati kuphunzira pang’ono pa Baibulo. Ife tinali kuyankhula za chikondi.

Ndipo panali munthu wina ananena kwa ine, iye anati, “Ine ndikukhulupirira kuti ndinu wotsutsakhristu.”

³⁷ Ine ndinati, “Ngati izo zikanakhala zokondweretsa kwa Ambuye wanga, ndicho chomwe ine ndikanafuna kuti ndikhale. Ine ndikufuna kuti ndikhale chirichonse chimene Iye akufuna kuti ine ndikhale. Ine ndimamukonda Iye. Ndipo ngati Iye angati andiponyere ine mu gehena, ine ndidzamukondabe Iye, ngati ine ndizipita ndi mzimu womweu ndi umene ine ndiri nawo tsopano.” Iye anayang’ana pa ine mokhala ngati mwachirendo.

Ine ndinawona anai kapena asanu a iwo pamene, anyamata; azikazawo aang’ono, akazi abwino. Ine ndimadziwa momwe anyamata awo amawakondera akazi awo, chotero ine ndinanena kwa iwo, ine ndinati, “Iyi ndi njira yomwe mungayesere izo. Ngati akazi anu, inu musanakwatirane. . . Tsopano, inu mupite mmbuyo, titi inu. . . moyo wam’ banja uwu, inu mukanakhala mukulota inu mutakwatirana; inu kwenikweni muli musanakwatirane, koma inu mumalota inu muli. Ndipo inu mutadzuka, ndipo inu munapita ndi kukayankhula izo kwa bwenzi wanu wamkazi, ndi kuti, ‘Iwe ukudziwa, ine ndinalota kuti ife tinali titakwatirana, ndipo ife tinali ndi ana. Ife tinali tikukhala mosangalala, ndipo—ndipo tinali tikuyembekezera Kudza kwa Ambuye, ndi chirichonse.’ Ndiyeno msungwana uyu akananena kwa iwe, ‘Iwe ukudziwa, ine ndikumukonda mwamuna wina bwinoko kuposa momwe ine ndimakukondera iwe. Ine ndikanamakhala wokondwa ndi mwamuna winayo.’ Kodi iwe ukanakhoza, kuchokera mu mtima wako, kumukonda iye bwino mokwanira ndi kuti, ‘Madalitso a Mulungu akhale pa iwe, wokonededwa wanga. Pita ndi mwamuna wina uyu?’”

Tsopano, tsopano fufuzani izo, aliyense wa amuna inu kapena akazi inu. Mukuona? Chabwino, ngati chikondi

chanu chiri cholondola, inu mukanati muchite izo, pakuti inu muli kukondweretsedwa ndi ubwino wake. Chimene, inu mukudziwa kuti inu mukanakhoza kukhala naye, inu mukanakhoza kumakhala naye, inu...Iye ndi mkazi wanu; iye adzakhala ali. Iye adzakwatiwa nanu, koma iye sadzakhala ali wokondwa. Iye akanadzakhala ali wokondwa...Ndiyeno, ngati inu mukumukonda iye, ndiye inu mukufuna iye akhale ali wokondwa.

Chotero, chirichonse chimene chiri chifuniro cha Mulungu, mulole chifuniro cha Mulungu kuti chichitidwe, kaya ine ndiri wokondwa nacho kapena ayi. Ine ndikufuna kuti ndizikhala mwakuti Iye azikhala ali wosangalatsidwa ndi zimene ine ndikuzichita. Chotero fufuzani chanu—chofuna chanu ndi cholinga chanu pa izo; inu mudziwa ngati inu mukumukonda Mulungu kapena ayi.

Bwanji ngati Iye akanati, “Iwe unditumikire Ine ngati Ine nditi ndidzakutayire iwe kunjya?”

“Ine ndizikukondani Inu, mulimonse.”

³⁸ Chotero, ngati mipingo ikanati iwone izo ndipo ikanakhoza kukhulupirira izo motero, izo sizikanakhoza kukhala mmodzi akuyesera kuti alande mpira kwa munthu winayo pamene iye akuthamanga ndi iwo. Iye akanakhala akumuteteza ameneyo. Mukuona? Pamene, cholinga choona chenicheni ndi chofuna, sizikanakhala wina akuyesera kuti, “Hei, ine ndiri ndi *ichi* inenso! Ine, *ichi* ndi ine, *ichi*.” Mwaona, Mulungu sangakhoze kumugwiritsa ntchito munthuyo. Pali zosanzira zochuluka kwambiri zimene zimatsatira izo, ndipo uyo ndi Satana. Ndipo anthu sangakhoze kuzindikira izo. Iwo akuyesera kuti atenge mpira kuchokera kwa wina yemwe wapatsidwa iwo. Musiye Mulungu adzutse utumiki winawake ndipo muwone ndi angati ati apite mofuna iwo. Mukuona? Mukuona?

³⁹ Tsopano, chikondi chenicheni kwa Mulungu, “Ziribe kanthu ndi gawo lanji lomwe ine ndiri, Ambuye, ngati ine ndingakhoze kungonena mawu a Ilo, kuthandiza kuwatetezera Iwo, ndiroleni ine ndichite izo.” Mukuona?

Ndicho chinthu chofanana chimene chingakhale chokhudza mkazi wanu. Ngati inu mumamukonda iye kwenikweni, mwaona, icho si—icho si—chikondi cha *phileo*; ndi chikondi cha *Agapao*, chikondi chenicheni. Iye akhoza kukakhala ndi munthu wina, mokondwerapo; inu simunakwatirane pano, ndithudi, inu simungakhoze.

⁴⁰ Ndipo, tiri chiyankhulire, anthu amene akumvetsera matepi awa. Ena, ochuluka kwambiri, akutumiza kuno, akuti, “Bwanji, mu *Chikwati Ndi Chilekano*, inu munanena *izi* ndipo inu munanena *izo*.” Ine ndimanena izo nthawi zochuluka kwambiri; matepi awa amapita kokha...ine ndikuyankhula kwa gulu langa, m’bale. Ine sindiri woyankhira zimene Mulungu

wakupatsani inu kuti mulishye; ine ndiri woyankhira pa mtundu wa Chakudya chimene ine ndikuwadyetsa anthu awa. Izi ndi za kachisi uyu yekha. Mukuona? Tsopano, ngati anthu akufuna kuti azimvetsera kwa matepi, izo ziri kwa iwo. Koma ine ndiri kuyankhula kwa amene Mulungu wawapereka kwa ine. Anali machimo awo amene anafutidwa.

Wina analemba, anati, “Chabwino, ine ndinachita *izi* ndipo ine ndinachita *izo*. Ine munati machimo athu. . .” Ine—ine sindimanena zimenezo.

Ine ndinati, “Penyani izo pa ichi; izi ziri kokha kwa anthu awa pomwe pano, anthu pano mu kachisi, nkhoa zanga zanga.” Tsopano, ngati anthu akufuna kuti azipanga haibridi chakudya ndi zinthu kunja uko, inu—inu kapezeni vumbulutso kuchokera kwa Mulungu ndipo kachiteni zimene Mulungu akuwuzani inu kuti muchite. Ine ndikachita chinthu chomwecho. Koma Mauthenga awa ali kwa mpingo uno.

⁴¹ Zindikirani tsopano, ife tibwerere mmbuyo, ife tiyenera kukhala ndi chinachake chimzake chimene ife tiyenera kugwirako. Chinachake chiyenera kukhala chiri chikhomo chomangapo, mwa kuyankhula kwina, ndi chochidalira. Ndipo aliyense ayenera kukhala ndi chochidalira kapena mtheradi. Ine ndinalalikira pa izo nthawi ina, zaka zapitazo, pa mtheradi, malo amene ali mawu otsiriza.

⁴² Monga woyimba kherere pa masewero a mpira, ngati iye anena kuti ndi kuponya, ndizo chimodzimodzi basi chimene izo ziri. Ziribe kanthu momwe inu mukuwonera izo, woyimba kherere wanena kuti ndi kuponya. Inu mukuti, “Ine—ine—ine. . .” Iko sikunali kuponya. Iwo unapita. . .ine ndinawuona. . .” Ziribe kanthu chimene chiri, pamene iye anati, “kuponya,” ndi zimenezo, izo zakhazika basi chimene. Iye, iye ndi chochidalira.

⁴³ Ndipo nyali za pa msewu ndi chochidalira, ngati izo ziti, “pitani.” Inu nkuti, “Chabwino, ine, ine ndiri kufulumira, ine ndiyenera. . .” Ayi, ayi. Izo zikuti, “Inu muyime njii pamene munthu winayo akupita.” Mukuona? Ndicho chochidalira.

⁴⁴ Tsopano, payenera kukhala chochidalira ku chirichonse chimene inu mukuchichita. Panayenera kukhala chochidalira pamene inu munkamusankha mkazi wanu. Pankayenera kukhala mkazi yemwe inu munkayenera kumusankha.

⁴⁵ Tsopano, payenera kukhala nthawi imene, pamene inu mukupita kukagula galimoto, ndi chochidalira cha mtundu wanji chimene inu muti mupange. Kodi icho chikhala Ford, Chevy, Plymouth, galimoto yakunja, chirichonse chimene iyo ili, inu muyenera kukhala ndi chochidalira.

Ndipo chotero izo ziri ndi kukhala kwa Chikristu. Payenera kukhala pali chochidalira.

⁴⁶ Tsopano, ngati munthu akanati, akanapita kwa munthu wina ndipo akanati...atamumva wina akuti, “Chabwino, inu muyenera kubatizidwa,” ndipo munthu uyu sana... Mwinamwake, ali, mpingo wina umene sumabatiza, iwo amangokonkha. Ine ndikuganiza, titi mwachitsanzo, Amethodisti, iwo amabatiza ngati izo zipemphedwa, ine ndikumva. Kapena mwinamwake... .

Akatolika, ine ndikuganiza iwo amakonkha kokha. Chotero ndiye ngati—ngati munthu anamva chinachake za “kumizidwa mu madzi,” chabwino, iye asali kumvetsa izo; iye analeredwa wa Chikatolika. Chotero iye akupita kwa ansembe, ndi kukati, “Bambo, ine ndikumva kuti ife timayenera kuti tizibatizidwa mwa kumiza. Kodi mpingo wathu umanena chiyani pa izo?”

⁴⁷ “Bwanji, iwo umanena kuti—kuti ife tizikhala tikukonkhedwa.” Ngati mpingo umenewo uli chochidalira chake, izo zikhazikitsa icho. Kukangana konse kwatha; mpingo wanena chomwecho, ndipo ndizo zonse.

⁴⁸ Bwanji ngati...ngati m'bale wa Chibaptisti atatimva ife tikunena kuti ife timakhulupirira mu kubatizidwa mwa “kumizidwa?” Iye akanati, “Ine ndimakhulupirira izo.”

“Ndipo mu Dzina la ‘Yesu Khristu.’”

Tsopano, uyu—membala uyu wa mpingo akabwerera kwa abusa ndi kukati, “Abusa, ine ndinamumva wina akunena kwa ine kuti ife tiyenera kubatizidwa mwa kumizidwa, nzolondola, koma mu Dzina la ‘Yesu Khristu.’”

⁴⁹ “Chabwino,” iye akanati, “tsopano, tiyeni ife tiwone. Bwanji, pano bukhu likunena kuti ife tizibatizidwa pogwiritsa ntchito ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera.’” Ngati mpingo umenewo uli chochidalira, izo zikhazikitsa icho. Iye sasamala chimene china chirichonse chinena; icho ndi chochidalira chake.

⁵⁰ Chabwino, chipembedzo chirichonse ndi chochidalira kwa okhulupirira ake.

Koma, kwa ine, ndi kwa iwo amene ine ndikuyembekeza kuti ine ndikuwatsogolera kwa Khristu, ndi mwa Khristu, Baibulo ndi chochidalira chathu. Ziribe kanthu... Chifukwa, Mulungu anati, “Siyani mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga Choonadi.” Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Baibulo ndi chochidalira cha Mulungu. Ziribe kanthu zimene wina aliyense anena; Ndicho chochidalira.

Baibulo si bukhu la machitidwe. Ayi, bwana. Ilo si bukhu la machitidwe, kapena mfundo za makhalidwe. Baibulo si bukhu la machitidwe, zochitika zochuluka kwambiri, ndi zina zotero. Ayi, bwana. Ilo si bukhu la makhalidwe. Ayi, bwana. Ilo sindilo. Ngakhale Ilo si bukhu la mbiriyakale, palimodzi. Kapena, ngakhale kuti Ilo si bukhu la zamulungu. Pakuti, Ilo ndi vumbulutso la Yesu Khristu.

Tsopano ngati inu mukufuna kuti muwerenge izo, inu amene muli ndi mapepala anu, mukuzilemba izo, ndi Chivumbulutso 1:1 mpaka 3, monga, Baibulo ndi “Vumbulutso la Yesu Khristu.”

⁵¹ Tiyeni ife tingoziwerenga izo pamene ife tiri nayo nthawi. Ine ndikukhulupirira zanga . . . ndiribe zolemba zambiri pano kuti ndiyankhule kuchokerapo. Ngati Ambuye achedwa, bwanji, ife tidzayesera kuti titenge kuchokera kwa izo.

Vumbulutso la Yesu Khristu, limene Mulungu anapereka kwa iye, kuti asonyeze kwa antchito ake zinthu zimene ziyenera kuchitika posachedwapa; ndipo iye anatumiza ndipo anazisonyezera izo ndi mngelo wake kwa wantchito wake Yohane:

Yemwe anachitira umboni wa mawu a Mulungu, ndi . . . umboni wa Yesu Khristu, ndi wa zinthu zonse zimene iye anaziwona.

Wodala ali iye amene awerenga, ndi iwo amene amva mawu a weneri wu, ndi kusunga zinthu zimene zalembedwa mmenemu: pakuti nthawi ili pafupi.

⁵² Chotero, Baibulo ndi vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu. Ndipo Ilo linalembedwa ndi aneneri. Ahebri 1:1, mu . . . “Mulungu, Yemwe mu nthawi zakale anayankhula kwa makolo mwa aneneri, mu tsiku lotsiriza lino akuyankhula kwa ife kupyolera mwa Mwana Wake, Yesu Khristu,” yemwe anali aneneri, onse a iwo, atayikidwa palimodzi. Yesu anali Malaki; Yesu anali Yeremia, Yesaya, Eliya. Zonse zimene iwo anali, zinali mwa Iye. Ndi zonse zimene inu muli, ndi zonse zimene ine ndiri, ziri mwa Iye; Mawu, mboni za Mawu.

Chotero Ilo si bukhu la zochitika, dongosolo la makhalidwe, kapena kuti Ilo ndi bukhu la mbiriyakale, kapena bukhu la zamulungu. Ilo sindilo ayi. Koma Ilo ndi vumbulutso la Yesu Khristu, Mulungu Mwiniwake akuwululidwa, kuchokera ku Mawu mpaka mu mnofu. Ndicho chimene Ilo liri. Baibulo ndi Mawu, ndipo Mulungu ndi thupi, Mulungu mwa . . . Mulungu ndi Mawu, kani, ndipo Yesu kukhala thupi. Ndilo vumbulutso, momwe Mulungu (Mawu) anawonetseredwa mu thupi laumunthu, ndipo anawululidwira kwa ife. Ndipo ndicho chifukwa Iye akukhala Mwana wa Mulungu; Iye ali gawo la Mulungu. Inu mukumvetsa? Tsopano, Iye sikuti ali . . . Thupilo liri gawo la Mulungu, mochuluka kwambiri kuti ilo ndi Mwana.

⁵³ Mwana, monga Akatolika amanenera izo, “Mwana Wamuyaya,” ndi mipingo ina yonse; mawuwo sakupanga konse zomveka. Mukuona? Sipangakhoze kukhala Wamuyaya, ndiyeno nkukhala Mwana, chifukwa *Mwana* ndi chinachake chimene “chinachita kubalidwa.” Ndipo mawu akuti Wamuyaya, Iye sangakhoze kukhala Wamu- . . . Iye akhoza kukhala Mwana, koma Iye sangakhoze kukhala Mwana Wamuyaya. Ayi, bwana. Iye sangakhoze kukhala Mwana Wamuyaya.

⁵⁴ Tsopano, koma Iye ndi Mwana, mochuluka chotero kuti, kuti Mawu onse amene anali mwa Yerima, mwa Mose, ndi Mawu onse amenewo, monga Iye anati, “Iwo amayankhula za Ine.” Vumbulutso lonse loona Laumulungu ilo la Mawu linamangidwa mu thupi limodzi laumunthu, ndipo Mulungu anayika mnofu mokutira Ilo. Ndicho chifukwa Iye ankatchedwa “Mwana,” nchifukwa Iye amakamba za, “Atate.” Bwanji, ndi zophweka basi, ngati inu mutangolola Mulungu kuti azitsanulire izo mu malingaliro anu. Mukuona? Mulungu atawululidwa mu thupi la mnofu, zindikirani, atawululidwa kuchokera mu mnofu... kapena kuchokera ku Mawu kupita mu mnofu. Ndizo Yohane Woyera 1:14, “Ndipo Mawu anasanduka thupi, ndipo anakhala pakati pathu.”

⁵⁵ Tsopano zindikirani Baibulo ili. Ena a iwo anati, “O, chabwino, Ilo linachita izi, Ilo linachita izo.” Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, tiyeni tingo...

Tiyeni tipite mu mbiriyakale ya Baibulo, miniti chabe, tiwone kumene Ilo linachokera. Ilo linalembedwa ndi olemba makumi anai osiyana. Anthu makumi anai analemba Baibulo, kupitirira danga la zaka mazana khumi ndi asanu ndi limodzi kutalikirana, ndipo pa nthawi zosiyana, akuneneratu zochitika zofunika kwambiri zimene zinayamba zachitikapo mu mbiriyakale ya dziko, ndipo, nthawi zambiri, zaka mazana izo zisanachitike. Ndipo mulibe cholakwika chimodzi mu Mabuku onse makumi asanu ndi limodzi mphambu asanu ndi imodzi. O, mai! Palibe mlembi koma Mulungu Mwiniwake angakhoze kukhala wolondola chotero. Palibe Mawu amodzi amatsutsana ndi ena.

Kumbukirani, kutalikirana zaka mazana khumi ndi asanu ndi limodzi, Baibulo linali likulembedwa, kuchokera kwa Mose mpaka—mpaka ku imfa ya—ya Yohane pa chisumbu, kapena Chisumbu cha Patmo. Zaka mazana khumi ndi asanu ndi limodzi, ndipo linalembedwa ndi olemba makumi anai osiyana; mmodzi sanali kumudziwa nkomwe winayo, ndipo iwo sanali nalo Ilo ngati “Mawu.” Ena a iwo sanawawone konse “Mawu.” Koma pamene iwo ankawalemba Iwo, ndipo iwo ankamvetsedwa kuti anali aneneri, ndiye, pamene iwo anayika mauneneri awo palimodzi, umodzi uliwonse wa iwo umalumikizana umodzi kwa umzake.

⁵⁶ Tayang’anani pa Petro, yemwe analengeza pa Tsiku la Pentekoste, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu.”

Paulo anali asanamve kalikonse za Izo. Iye anapita ku Arabia kwa zaka zitatu, kuti akachiphunzire Chipangano Chakale, kuti akawone Yemwe Lawi la Moto ili anali yemwe anayankhula kwa iye pa njira, kuti, “Saulo, chifukwa chiyani

iwe ukundizunza Ine?” Iye akanakhoza kukhala akulakwitsa motani? Iye sanakawufunse mpingo nkomwe.

Ndipo zaka khumi ndi zinai mtsogolo, pamene iye anakomana ndi Petro, iwo anali akulalikira chinthu chofanana, Mawu ndi Mawu. Ndilo Baibulo lathu. Mulole mawu a munthu wina alephere. *Ili*, palibe munthu angakhoze kuwonjezera kwa Ilo. Inu simumawonjezera zinanso kwa Baibulo. Ayi, bwana. Ili ndi Vumbulutso lathunthu. Ndizo zonse.

⁵⁷ Monga Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. “Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri,” wina anapitirira kumanena kwa ine, “tsopano inu mudza . . . Ambuye adzayankhula kwa inu, M’bale Branham, pamene Zisindikizo izi zidzawululidwa, ndipo mudzatiuza ife momwe tingayandikirire kwa Mulungu, ndi momwe tingachitire izo.”

⁵⁸ Ine ndinati, “Ayi, bwana, izo sizingakhoze kukhala. Chifukwa, Baibulo, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri pa Ilo zinali zitabisa zinsinsi zisanu ndi ziwiri. Izo zinali zitalembedwa kale, koma iwo sanali kuzimvetsa chomwe Izo zinali.”

Yang’anani momwe iwo anatipulira limodzi ndi izo, kubatizidwa mu Dzina la “Yesu”; mukuona, izo sindizo. Dzina la “Ambuye Yesu Khristu”! Mukuona zinthu zonse izo, momwe izo zinaliri. Chifukwa, alipo a Yesu ochuluka; ine ndiri nawo amzanga angapo pano pa dziko lapansi otchedwa “Yesu,” amzanga otumikira. Si zimenezo ayi. Ndi “Ambuye Yesu Khristu” wathu.

Palibe mlembi wina koma Mulungu angakhoze kukhala wolondola kwambiri. Tsopano tiyeni tingowona momwe Baibulo ili linalembedwera.

⁵⁹ Tsopano, tinene mwa chitsanzo, kuchokera . . . Bwanji ngati ife tikanapita tsopano ndipo tikanakatenga mabuku azamankhwala makumi asanu ndi limodzi mphambu asanu ndi imodzi amene amachita nalo thupi, olembedwa ndi masukulu azausing’anga makumi anai, zana ndi khumi ndi zisanu ndi chimodzi . . . kapena kutalikirana zaka mazana khumi ndi zisanu ndi chimodzi? Ndikudabwa kuti ndi kugwirizana kwa mtundu wanji kumene ife tikanati tibwere nako?

Pamene, George Washington, purezidenti wathu, pafupi zaka mazana awiri zapitazo, chifukwa cha chibayo, iwo anamuchotsa chikhadabo chake ndi kumukhetsa iye painti. Bwanji ngati ife tikanatenga . . .

⁶⁰ Tiyeni tipite patsogolo pang’ono, pa zinthu zina zimene ife timakopedwa nazo kwambiri lero, ndizo sayansi. Bwanji ngati ife tikanatenga sayansi makumi anai zosiyana, kuchokera ku kutalikirana kwa zaka mazana khumi ndi zisanu ndi chimodzi, ndipo tiwone chimene ife tingabwere nacho? Wa sayansi wa Chifrenchi, zaka mazana atatu zapitazo, anatsimikizira mwa

sayansi, pa kugudubuza mpira, kuti, ngati liwiro lowopsya lirilonse litapangidwa kupitirira mailosi makumi atatu pa ora, chinthucho chikanakhoza kusiya dziko lapansi ndi kugwera kwina. Kodi inu mukuganiza kuti sayansi inganene za izo? Kodi pali kugwirizana kulikonse ndi izo tsopano, pamene iwo akuyendetsa mu msewu, pa msewu kuno, mailosi zana ndi makumi asanu pa ora? Mukuona? Koma iye anatsimikizira mwasayansi izo, mwa mpweya wa mpira ukugudubuzika pansi, kuti pa mailosi makumi atatu pa ora, kuti, chinthu chirichonse chikhoza kunyamuka kuchoka pa dziko lapansi ndi kupita kwina, chikanati chikagwere kwina mu mlengalenga. Ayi, palibe kupitirizika kwa izo.

⁶¹ Koma palibe Mawu amodzi mu Baibulo amene amatsutsana ndi enawo. Palibe mneneri mmodzi yemwe anayamba watsutsana ndi mzake wina. Iwo anali, mmodzi aliyense, mwangwiro. Ndipo pamene wina abweramo ndi kudzanenera, ndipo mneneri weniweni uyo ankawuka ndi kumuitanira apo iye, ndiye izo zinali kuwonetseredwa. Mukuona? Mukuona? Chotero Baibulo ndi Mawu a Mulungu, kwa okhulupirira mowona onse.

⁶² Tsopano, inu simukanakhoza kupeza kulondola kulikonse mu zimene asing'anga amagwirizanapo. Inu simungakhoze ngakhale kupeza kulondola kwa iwo tsopano. Inu simungakhoze kupeza kulondola mu sayansi tsopano.

Tsopano, inu mukudziwa, nthawiyina kale, iwo anatiuza ife kuti. . .kuti, “Pamene Baibulo linanena kuti ‘iye anawona Angelo anai ataima pa ngodya zinai za dziko lapansi,’ kuti izo sizikanakhoza kukhala choncho. Dziko ndi lozungulira.” Koma Baibulo linati, “ngodya zinai.” Chabwino, tsopano inu munawona, masabata awiri apitawo, kapena masabata atatu apitawo, izo zakhala ziri tsopano, mapepala alembamo nkhani iyi, iwo apeza kuti dziko ndi lamphwamphwa. Ndi angati anaziwona izo? Bwanji, zedi. Mukuona? Ine ndinakopa zonse izo, ndikungoyembekezera kuti wina anene chinachake.

⁶³ Ndipo iwo adzapeza, tsiku lina, kuti iwo sakuwona zaka mamilioni zana ndi makumi asanu za kuwala mu mlengalenga nkomwe. Iwo akupita kumene chozungulira mwa mkombero. Ndizo ndendende.

Inu mudzapeza, limodzi la masiku amenewa, kuti pamene inu mupita Kumwamba, inu sumuwulukira kwina kwake. Inu mumangokhala komwe kuno, naponso, mu chikhalidwe china chokha chaliwiro kuposa chino.

Kudutsa mu chipinda chino chomwe ukubwera mtundu. Mtundu uliwonse, malaya, diresi, chirichonse chimene inu mwavala, ndi Chamuyaya, ziri pa rekodi yomwe, zikuzungulira zungulira dziko. Nthawi iliyonse imene inu mukuphethira

maso anu, izo ziri pa rekodi yomwe. Penyani, televizioni itsimikizira izo.

⁶⁴ Pamene iwe ubadwa, Mulungu amayambitsa rekodi. Izo sizimapanga... Amayambitsa rekodi, iyo simapanga phokoso lochuluka kwa kanthawi pang'ono, inu mukudziwa. Ameneyo ndi mwana wamng'ono, mpaka iye akafika pa kuzindikira; ndiye phokoso limayamba, iye amayamba kunena zinthu ndi kuchita zinthu zimene iye ayenera kuti adzakayankhire. Ndiyeno pamene moyo uwo utha, rekodi imeneyo kapena tepi imachotsedwapo ndi kukaikidwa mu—nyumba yosungira yayikulu ya Mulungu. Tsopano, inu mukuti mukalambalala motani izo pa Malo a Chiweruzo? Izo zikuseweredwa mobwereza patsogolo panu pomwe, kusuntha kulikonse kumene inu munakupanga, lingaliro lililonse limene linadutsa mmalingaliro anu. Kodi inu mukukhoza kuziwona izo? Tsopano kodi inu mungakhoze kuwona kumene Mulungu. . .

⁶⁵ Nditaima pano usiku wina, ndipo kunali munthu pa nsanja, wamtali, mwamuna wa mutu-wadazi, munthu wowoneka-mokongola kwenikweni, wamphamvu. Ndipo iye anatuluka. . . Ambuye anali atamuza iye zambiri zonse zokhudza banja lake ndi chimene iye ayenera kuchita. Ndipo iye anatuluka ndipo anakakhala pansu. Mu maminiti pang'ono, anabwera patsogolo pa ine mwamuna wina wonga ameneyo, koma iye anali ndi mutu wake atawerama. Ine sindimakhoza kumuzindikira, ndipo ine ndinayang'ana pa bamboyo kachiwiri kunja uko; ndipo iye. . . Sanali iye, chifukwa icho chinali chinachake. Ndipo munthu uyu, ine sindimakhoza kumupeza. Ndinayang'ana pozungulira, kunalibe wina kumbuyo kwa ine. Ine ndinati, “Bamboyo wakhala mkati mwa makatani awo uko.” Ndipo uyo anali wathu. . . m'bale yemwe amabwera ku mpingo kuno, wamtali, wamutu-wadazi, munthu wokhala ngati wokongola atakhala pamwamba apo monga choncho. Ndipo iye anali atazolikitsa mutu wake, akupemphera, chifukwa iye anali pafupi kuti afe ndi vuto la mmimba.

Iye ankati akagule nsapato zina. Mkazi wake ankafuna kuti iye akagule nsapato zatsopano. Iye anati, “Ayi, ine sindikusowa kuti ndikagule izo, chifukwa ine sindikhala moyo kuti ndizivala izo.”

Iye anali akufa. Ndipo atakhala pamenepo, inu mukuona, mu malo enawo, aleluya, Mulungu anangosunthira pamenepo ndipo anati, “Ndi uyo wakhala apoyo,” basi momwe iye analirimo. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

⁶⁶ Tsopano zindikirani, ndipo mulibe kulakwitsa kulikonse mu Malemba. Yesu, Mawu a Mulungu, amazindikira maganizo omwe ali mu mtima. “Mawu a Mulungu ndi amphamvu, othwerapo,” Ahebri 4:12. “Mawu a Mulungu ndi othwerapo, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse,

ngakhale ozindikira malingaliro ndi zamkati mwa malingaliro.” Mukuona? Amapita mpaka pansi mu malingaliro, ndi kusololera kunja, ndipo amazindikira. Kodi *kuzindikira* ndi chiyani? “Kupangitsa kudziwika, kuwulula poyera.” Ndipo ndicho chimene Mawu a Mulungu amachita.

Lero ife timati, “Mpingo wa Katolika ndiwo Mawu a Mulungu; wa Chibaptisti, wa Chimethodisti, wa Chipentekoste, kachisi.” Ndi kulakwitsa. Mawu ndiwo vumbulutso; Mulungu, kuwululidwa mwa Mawu.

⁶⁷ Ayi, ife tikanakhoza kukhala nako...kukhala nako kupitiriza kulikonse pakati pa azamankhwala, pakati pa asayansi, osiyana.

Ngati Einstein akanakhala nako kokha kuchita kwauzimu, monga iye anali—ndi kuchita kwathupi, pamene iye anali kuphunzira malamulo a kuwala, ndi zina zotero, iye akanakhoza kutiuza ife chinachake. Pamene ine ndinamva uthenga wake wa chirikati chachikulu chija kwinakwake mu milengalenga, kuti, “Yense yemwe angakhudzane ndi chirikati chimenecho, iwe ukanakhoza kulenga maiko, kuchita chirichonse, ndipo mphamvuyo ikanakhala yopanda malire.” Mukuona? Iye anali ataziwona izo.

⁶⁸ Inu mukuona timatumba tating’ono iti timene tikumayenda kudutsa mu mpweya, iwo akuzitcha “mbale,” zina zotero. Anthu chotero...Kuti, chabwino, ife kulibwino tizisiye izo zokha. “Mukumva za anthu onse awa amene akumasowa?” inu mukuti. Osamvanso za iwo; iwo amayima pamenepo, ndipo iwo nkukhala palibe.

Ndi momwe Mkwatulo uti udzakhaliro. Chimodzi cha izo chidzagwera pansi, ndipo thupi ili lapansi pano lidzavala thupi lakumwamba. Ndipo iwo adzakhala...chikopa, tsitsi, kapena mafupa zitatsala; ilo lidzakhala litasinthidwa mu kamphindi ka nthawi, kubwera kuchokera mu mlengalenga momwe ndi kulitengera kwathu ilo. Ife tikuziwona zonse izi zimene zikuchitika tsopano, ndipo—ndipo Pentagon ikudabwa nako kuwala uku, ndi kuwala kwachinsinsi, ndi chirichonse chimene iwo akuchiwona mu—mu mlengalenga. Inu mukuona iwo anali nacho chimodzi kuno mu pepala ku Jeffersonville sabata ino, ndi zina zotero, “kuwala kwachinsinsi.” Chotero, o, iwo sakudziwa chomwe izo ziri. Koma mveterani, ana aang’ono, Icho chidzakunyamulani inu, limodzi la masiku awa. Mukuona? Mukuona? Musati mudandaule.

Kumbukirani, Yesu anati, “Monga izo zinali mu masiku a Sodomu.”

⁶⁹ Nchiani chinachitika basi asanati Sodomu? Mulungu anabwera pansi ndi Angelo ena, ndipo iwo anali ndi kufufuza kwa chiweruzo. Anati, “Ine ndamva kulira, kuti ndi kochimwa kwambiri, kwakukulu kwambiri, chotero ine ndatsika kuti

ndidzafufuze ngati izo ziri palimodzi zoona kapena ayi.” Kulondola uko? Muyang’aneni wamkulu Uja yemwe anatsalira ndi Abrahamu, ankakhoza kuzindikira malingaliro amene anali mu mtima mwa Sarah, kumbuyo kwa Iye.

Tsopano, inu muyang’ane pozungulira pang’ono pokha ndi kuzindikira, kuwona, kuyang’ana chimene Iwo akuchita, chinthu chomwecho lero. Ndiko kufufuza chiweruzo.

Bwanji, patapita kanthawi, Mpingo, pamene Iwo ungakhoze kukhala mu malo amenewo, ndipo mbewu iliyonse ikabweretsedwa pa malo ake, iwo adzakhala atapita. Iwo sadzadziwa chimene chachitika kwa iwo. Wina adzakhala akupita mbali ina. Mukuona? Wina adzakhala akupita ku nyumba ya abusa, ndipo wina adzakhala akupita *uku*, kapena kumusi *uko*, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo kulibe uko. Pakuti Enoki yemwe anali choyimira, “Mulungu anamutenga iye, ndipo iye sanapezekenso.” Akubwera pansi kuti adzafufuze! Kugwirizana, momwe kusinthika kwa Enoki, choyimira. Cha Israeli kukhala atatengedwera kwinako mu chombo . . .

⁷⁰ Zangwiro kwambiri, Mawu a Mulungu ndi angwiro kwambiri, ngakhale kwa Chipangano Chakale ndi Chatsopano, ndi matheka awiri ndi thunthu limodzi. Ndiko kulondola. Chipangano Chakale ndi theka la Iwo, ndipo Chipangano Chatsopano ndi theka la Iwo; mukayika Iwo pamodzi, inu mukhala ndi vumbulutso lonse la Yesu Khristu. Uko kuli aneneri akuyankhula, ndipo kuno Iye ali mwa Umunthu; mwaona, matheka awiri ndi thunthu limodzi. Tsopano ife sitikufuna kuti titenge mochulukwa kwambiri . . .

⁷¹ Tsopano, kumbukirani, Chipangano Chakale sichimakhala champhumphu popanda Chatsopano. Ndipo Chatsopano sichingakhoze kukhala champhumphu popanda Chakale. Ndicho chifukwa ine ndinati matheka awiri, thunthu limodzi. Pakuti, aneneri anati, “Iye adzabwera kuno! Iye adzabwera kuno! Iye adzabwera kuno; iwo adzachita *izi* kwa Iye. Iwo adzachita *izi* kwa Iye!” Ndipo ndi Uyu apa, “Iye anali kuno! Iye anali kuno, ndipo iwo anachita *izi* kwa Iye, ndipo iwo anachita *izi* kwa Iye.” Ine ndalalikira posachedwapa pa izo mausiku angapo apitawo.

⁷² Tsopano, polinga kuti tiwaphunzire Malemba, Paulo anamuuzza Timoteo, “Phunzira Iwo, uziwagawaniza molondola Mawu a Mulungu, amene ali Choonadi.”

Izo ndi zoyenera zitatu mu Lemba. Pa kugwiritsa ntchito Mawu a Mulungu, pali zinthu zitatu zimene inu muyenera kuti musamachite. Tsopano tiyeni tiphunzire izo kwa maminiti ena khumi; zinthu zitatu zimene inu simumayenera kuti muzichita. Ndipo nonse kunja mu dziko, kulikonse kumene inu muli, ku fuko lonse, khalani otsimikiza kuti muzilembe izi mu

malingaliro anu ngati inu mulibe cholemba. Inu muyenera kuti musamachite zinthu izi. Ife timakuuzani inu nthawizonse momwe inu muyenera kumachita, tsopano ine ndati ndikuuzeni inu zimene inu muyenera kuti musamazichite.

⁷³ Tsopano, inu muyenera kuti *musamathanthauzire molakwika* Mawu. Inu mukuti, “Chabwino, ine ndikukhulupirira Iwo akutanthauza *ichi*.” Iwo amathanthauza chimene Iwo akunena basi. Iwo samasowa wotanthauzira wina. Ndipo inu muyenera kuti *musamayike polakwika* Mawu. Ndipo inu muyenera *musamasemphanitse* Mawu. Ndipo ngati ife tikanati tichite chirichonse cha izi, izo zimaponyera Baibulo lonse mu chisokonezo ndi mu chiwawa.

⁷⁴ Zindikirani. Kuti mumutanthauzire molakwika Yesu, mu mawonekedwe a Mulungu mwa munthu, inu mungati mumupange Iye—inu mungati mumupange Iye Mulungu mmodzi mwa atatuwo. Kuti mutanthauzire molakwika Yesu Khristu pokhala Mawu, inu mukanati mupange Iye Mulungu mmodzi mwa atatu, kapena inu mukanati mumupange Iye Munthu wachiwiri mu Umulungu. Ndipo kuti muchite izo, inu mukanati musokoneze Malemba onsewo. Inu simungakhoze kufika kulikonse. Chotero Iwo sayenera kuti azitanthauziridwa molakwika.

⁷⁵ Ndipo ngati inu munena kuti chinthu china, inu mutayika kutanthauza pa Iwo, ndipo inu nkuwayika Iwo ku nthawi ina; kapena Iwo kukhala atayikidwa ku nthawi ina, inu mukupanganso kutanthauzira kosalondola.

⁷⁶ Ngati aliynse atanthauzira molakwika Yesu Khristu mu Baibulo, kuti sali Mulungu Mwiniwake, kumupanga Iye Munthu wachiwiri, kapena Mulungu mmodzi mwa atatuwo, izi zikanati zisokoneze Mawu aliwonse mu Baibulo lonse. Izo zikanati ziswe lamulo loyamba, “Iwe usakhale ndi mulungu wina aliynse patsogolo pa Ine.” Chabwino. Izo zikanati zipange mtundu wonse wa Chikhristu gulu la opembedza mwachikunja opembedza amulungu atatu osiyana. Mukuona mtundu wa Baibulo limene inu mukanati mukhale nalo? Ndiye izo zikhoza kutipanga ife chimene Ayuda amati ife tiri. Amati, “Ndi uti mwa amulungu amenewo ali Mulungu wanu?” Mukuona? Chotero, inu mukuona, inu simungakhoze. . . Inu musati muzitanthauzira molakwika Baibulo.

Pakuti, Yesu Iyeyekha ali kutanthauzira kwa Baibulo, pamene Iye awonetseredwa mu m’badwo womwe gawo la Thupi Lake liri nkuwonetseredwa. Ngati iwo uli m’badwo wa dzanja, ilo liyenera kukhala dzanja; iwo sungakhoze kukhala m’badwo wa mutu. Ngati iwo uli m’badwo wa liwu, chabwino, ndiye, iwo sungakhoze kukhala m’badwo wa phazi. Mukuona? Ndipo tsopano ife tiri pa m’badwo wa diso. Ndipo tsopano chotsatira, ndi Iye Mwiniwake, kuti abwere. Kupenya; mwauneneri!

⁷⁷ Mwaona, mmusi kupyola mu m'badwo, ife tinayambira ku maziko, kuchokera ku m'badwo wa mpingo woyamba; pamene Mbewu inapita mu nthaka, Mbewu yathunthu. Ndiye iyo inatulukira kupyolera mu mapazi, Lutera; inabwereranso ndiye kupyolera mwa Wesile; ndiye mpaka kwa Achipentekoste, malirime, pa milomo, mukuona; tsopano izo ziri mu maso, uneneri, wa Malaki 4, ndi zina zotero. Ndipo tsopano palibe chinanso chimene chatsalira kuti chibwere koma Iye Mwiniwake kuti alowe umo, chifukwa ndicho chinthu chotsiriza chimene chiripo.

Chotsatira ndi luntha, ndipo ife tiribe luntha lathu lathu; ndi Lake. Ife tiribe kupenya kwathu kwathu. Munthu angakhoze bwanji kuwoneratu zinthu zimenezo? Iye sangakhoze kuchita izo. Ameneyo ndi Mulungu Mwiniwake. Mwaona, izo—izo zikufika pa malo. Ndipo Iye akulilamulira thupi njira yonse modutsa, ndiye Thupi lathunthu la Khristu liri kuwululidwa mwa mawonekedwe a Mkwatibwi yemwe anatengedwa kuchokera ku mbali Yake, monga Adamu anachitira pa chiyambi . . . monga Adamu anali, kani, pa chiyambi.

⁷⁸ Inde, “mulungu,” izi zikanati ziyike Baibulo lonse mu chisokonezo, kuswa lamulo loyamba, ndi kumupanga mulungu, mulungu wachikunja wa atatu. Izo zikanangoti—izo zikanati zisokoneze chithunzi chonse cha Baibulo. Chotero inu kuti musamatanthauzire molakwika Baibulo. Tsopano, icho ndi chinthu chimodzi chokha.

⁷⁹ Pamene, Lemba lirilonse mu Baibulo liri ndi kagwiritsidwe kofanana, inu muyenera kuliyika Ilo mu malo Ake. Ndipo kuliyika Ilo polakwika, inu mukhoza kumupanga Iye Mulungu mu m'badwo umodzi, ndi—ndipo m'badwo wotsatira inu nkumupanga Iye mbiriyakale, kuti uwayike polakwika Iwo. Chotero inu muyenera kuti musamayike polakwika Lemba. Iye ndi Mulungu nthawizonse. Ngati inu mutamupanga Iye lero Mulungu wa mbiriyakale, chimene iye anali mmbuyo kutali, ndipo Iye sali yemweyo lero, inu muchita naye chiyani Ahebri 13:8? Mwaona, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

⁸⁰ Tsopano, chotero mukuona zomwe ichi chikanati chichite, ndi chimene icho chachita. Izo zachita kale icho, kumupanga Iye kuwakana Mawu Ake Omwe, kuwayika polakwika Malemba.

⁸¹ Kutu muwasemphanitse Malemba, inu mukhoza kuyika thupi Lake palimodzi molakwika, phazi pamene mutu umayenera kukhala uli, kapena chinachake. Mofanana basi monga . . . Mwakuyankhula kwina, inu mukhoza kukhala ndi Yesu akuphunzitsa uthenga wa Mose. Inu mukhoza kukhala . . . kapena ngakhale Wesile akuphunzitsa m'badwo wa Lutera. Inu mukhoza kukhala nawo tsopano, m'badwo wathu, ukuphunzitsa Chipentekoste, uthenga wa Chipentekoste. Inu mukuona

chisokonezo chomwe Iwo akanakhala alimo? Chipentekoste chinasonyeza kale mangamanga ake. Lutera anasonyeza kale ake, anasochera anapita mu chipembedzo. Iwo unafera pomwepo. M'badwowo unagunda; pamenepo iwo unapita.

⁸² Zindikirani, mwamsanga basi pamene iwo unapangidwa bungwe, iwo unafa. [M'bale Branham akukhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.] Tsopano, tangoonani ngati izo siziri zolondola. Yang'anani mmbuyo kupyola mu masamba a mbiriyakale. Nthawi iliyonse imene iwo unapanga bungwe, iwo umafa pomwepo; sipamakhala chinanso kwa iwo. Iwo umakhala—wopembedza wa mulungu wa dziko lino, ndipo umapita mosochera mu zopangidwa, ndi mabungwe, ndi zipembedzo, ndi zinyengo. Gulu la ma Rickey analowa mmenemo ndipo anayikamo zolinga zawo mwa iwo, kapena kubayiramo malingaliro awo awo, kani, mwa iwo. Ndipo kodi ndi chiani chinachitika? Iwo umakhala nyansi. Ukathera mwa mulungu wa dziko lino, kumene iwo ati akamupatse mpandowachifumu Satana mwiniwake, kumaganiza kuti iwo ali ndi mtsogoleri wamkulu wa dziko woti awabweretsere iwo mtendere.

⁸³ Ine ndinakuuzani inu tsiku lina, ine ndikunena izo kachiwiri, kuti ngakhale chitukuko pa chokha lero chiri mwamtheradi chosiyana ndi Mulungu. Chitukuko chiri chosiyana ndi Mulungu. Maphunziro ali mailosi milioni kuchokera kwa Iye; sayansi ili mailosi milioni. Sayansi ndi maphunziro zikuyesera kuti zitsimikizire momutsutsa Mulungu, mwaona, kupyolera mu maseminare azamulungu ndi masukulu, ndi zipinda za sayansi, ndi zina zotero. Iwo akhala ali nako kugwedeza kwawo.

Nanga bwanji masomphenya usiku wina uja, a munthu pamene iye anafuula kwa asayansi kumusi uko akutsanulira zinthu zija umo monga choncho? Iwo anangopotoloka ndipo anayang'ana mmwamba, ndipo anapitirira. Padzakhala kukwera kwinsano kumodzi.

⁸⁴ Zindikirani, o, zoyenera zitatu izi ziyenera kukhala. Tsopano, inu simungakhoze... Yesu sanabwere akulalikira uthenga wa Nowa. Iye sanabwere akulalikira uthenga wa Mose. Kapena, Mose sanabwere akulalikira... Mwaona, musati musephanitse Malemba. Iwo ayenera kukhala mu nthawi. Tsopano, inu simungakhoze kugwiritsa... Pamene munthu wamkulu uja, Joni Wesile, anatulukira, kapena...

Munthu wamkulu, Lutera, pamene Lutera anatulukira ndi uthenga wake wa kulungamitsidwa. Tsopano pamene izo zinali... Lutera anali mwamuna wamkulu. Iye anauyitana mpingo kuchokera ku mdima, ndipo iye anakhazikitsa kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro. Ndipo pamene iye anachita izo, iwo anamanga chipembedzo pamwamba pa izo, ndipo iwo unafa. Moyo unayenda, monga iwo umakhalira mu phesi la tirigu, kupita mpaka mu m'badwo wa Wesile, mpaka

ngayaye. Kuchokera mwa Lutera munabwera masamba ena, amene anafa ndi iye, amene anali Zwingli, ndi Calvin, ndi ena onse amene anatuluka kuchokera mu kukonzanso kwakukulu kuja.

⁸⁵ Ndiye motsatira kunadza Wesile, m'badwo wina unali utaphukira kukhala ngayaye. Wesile, ndi Atterbury, ndi iwo onse, ndi—ndi Joni ndi m'bale wake, ndi onse a iwo, amuna aakulu a Mulungu ndi uthenga, anangolisesa dziko. Iwo anaupanga bungwe iwo; iwo unafa.

Ndiye iwo unatulukira ukuwoneka chimodzimidzi basi ngati kuti iwo unali kupita kukabala njere tsopano, ndipo, anafika podzapeza kuti, anali mankhusu, Pentekoste.

Koma kumbuyo kuseri kwa izo zonse, kunadza kamphukira kakang'ono.

Ndipo inu mukuzindikira, kawirikawiri. . . ine ndikuganiza, mwa pafupi zaka zitatu kapena zinai pambuyo pa Lutera ali mu utumiki, kuti mpingo wa Lutera unapanga bungwe. Nthawi yayifupi basi pambuyo pa Wesile ali pa utumiki, iwo unapanga bungwe.

⁸⁶ Tucson, ife tinali nalo—dongosolo la momwe mpingo wa Chiwesile, kapena mpingo wa Methodist, unafika pokhalapo. Ndipo pamene iwo anabwera ku Amereka kuno, ambiri a iwo anali atabwerera ndipo anati iwo anali atakonzana—chilolezo ndi zina zotero, kuchokera ku England, kuti awubweretse iwo kuno, ndi momwe izo zonse zinkachitidwira mwa seweru. Ine ndinachiwona apo pomwe chimene chinachitika. Pamenepo iwo unafa.

⁸⁷ Chabwino, panabwera Achipentekoste, ofuula akale aja mu masiku akutali kale, anali ndi mphatso za kuyankhula mu malirime, ndipo anayamba ndi kuyankhula mu malirime. Ndiye iwo anazitcha izo, “umboni wa Mzimu Woyera.” Ndiye iwo anapanga bungwe. Mmodzi amati iye akuti achite *izi*, ndipo wina *izo*, ndipo iwo anali ndi zinkhani ndi zinkhani. Kodi izo zinachita chiani? Lirilonse la masamba amenewo linali kumangofunyululuka, mofanana basi monga izo zinkachita mu phesi ndipo monga izo zinachita pa ngayaye. Iwo anali nawo umodzi, uwiri, utatu, ndi mpingo wa Mulungu, ndi ena onse awa; kumangofunyululuka, funyululuka, funyululuka.

Koma tsopano, malingana ndi chilengedwe, chimene chiri chitsanzo changwiro, inu simudzakhala konse chirichonse kuti muwaphunzitse Iwo achoke mu icho.

⁸⁸ Banja, la abwenzi anga uko mu Kentucky, anali atangokhala ndi wamng'ono—mwana wamng'ono atabadwa tsiku lina, ndipo mayiyo anali pamenepo pamene iwo anali akuphika chakudya chathu. Ndipo iye anali akumuthandiza mlongo wina kuphika chakudya cha gulu la amuna ife amene tinali kokasaka.

Ndipo chotero mwanayo anayamba kulira, ndipo ine ndinali kuyankhula. Ine ndikuganiza mayiyo anachititsidwa manyazi pang'ono, chotero iye anathamanga ndipo anakamutenga mwanayo, ndipo—ndipo anayamba ku—kumudyetsa mwana wamng'onoyo. Ine ndinati, “Inu mukudziwa, icho ndi chibadwa basi.” Mukuona? Tsopano, inu simungakhoze. . .

Iwo sanapeze konse njira yabwinoko iliyonse kuti mwana azipezera chimene iye akuchifuna kuposa kulirira icho. Tsopano, inu mukhoza kumupatsa iye—bukhu la makhalidwe, ndi kumukhazika pansu apa ndi kuti, “Ine ndikufuna kuti ndikuphunzitse iwe zamulungu, mwananga. Tsopano, iwe usati uziliralira pano monga ana ena; ndiwe wosiyana. Tsopano, pamene iwe ukufuna kuti udyetsedwe, iwe uziliza kabelu kakang'ono aka apa.” Sizingagwire ntchito basi. Ayi, izo sizingagwire ntchito basi.

⁸⁹ Chotero, pamene inu muyang'ana chilengedwe, tsopano ife tikuwona pamene m'badwo uliwonse, ndipo molunjika anazikonza izo kuti ife tiri mu m'badwo wotsiriza. Mankhusu achokapo. Ndipo ife takhala nazo zaka khumi ndi zisanu, pafupi makumi awiri tsopano, zaka, za Uthenga ukusesa kudutsa kuchokera ku fuko kupita ku fuko, ndipo mmawa uno talumikizidwa kudutsa fuko lonse lino, mwaona, ndipo palibe bungwe. Iwo sungakhoze kupanga bungwe. Sipanayambe pakhala kanthu kanayamba kakhalapo monga iwo, kapena kati kadzakhalepo pambuyo pathu. Mukuona?

Chi—chinthu chomwe chiri nkhani ndi Uthenga lero, ndi, iwo amene awulandira Iwo mu mitima yawo ayenera kuti azikhala mu Kukhalapo kwa Mwana, kuti afike pakucha. Mukuona? Iwe ukhoza kuwutenga Uthenga, ndiyeno nkulola Mwana awotchese chiwisi chonse chichoke mwa iwe, kumupanga Iye Mkristu wokhwima. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mulungu akubwera posachedwa, kuti adzaulandire Mpingo Wake, ndipo ife tiyenera kukhala nawo mtundu umenewo wa Akristu kuti Iye adzawalandire. Ti—tirigu ayenera kuti ache. Chabwino.

⁹⁰ Zoyenera zitatu izi ziyenera kukhalapo. Simuyenera kuti mutanthauzire molakwika, kapena kuugwira molakwika Iwo, kuwutanthauzira molakwika Iwo, kapena ku-. . .kapena kuwusemphanitsa Iwo. Iwo uyenera kuti usungidwe ndendende basi momwe Mulungu ananenera kuti unali.

Kwa dziko, Ilo ndi Bukhu la chinsinsi. Anthu amakhulupirira kuti Ilo ndi Bukhu lazachinsinsi chabe. Nthawi imodzi ine ndinali kuyankhula ndi munthu wotchuka kwambiri muno mu mzinda, yemwe wagwira maimidwe aakulu a Chikristu, ndipo iye anati, “Ine ndinayesera kuti ndiwerenge Bukhu la Chivumbulutso usiku wina.” Anati, “Yohane ayenera

kuti anali atakhuta ndiwo za tsabola wambiri wowawa ndipo iye anali ndi maloto oyipa.” Mwaona, Bukhu la chinsinsi.

⁹¹ Koma, pamene kwa wokhulupirira woona, Ilo ndi vumbulutso la Mulungu kukhala akuwululidwa mu m’badwo umene ife tiri kukhalamo. Iye anati, “Mawu Anga ali Mzimu ndi Moyo.” Yesu ananena zimenezo. Kachiwiri, “Mawu ali Mbewu zimene wofetsa anazifetsa.” Ife tikudziwa kuti izo ndi zoon. Ndi Mulungu mwa mawonekedwe a Mawu, ndipo akhoza kutanthauziridwa ndi Mwiniwake yekha.

Malingaliro aumunthu sali okhoza kuti atanthauzire malingaliro a Mulungu. Angakhoze bwanji aang’ono—malingaliro aang’ono amalire kutanthauzira Malingaliro opandamalire, pamene ife sitingakhoze ngakhale kutanthauzira malingaliro a wina ndi mzake?

⁹² Ndipo inu zindikirani, Iye ndi Mmodzi yekhayo angakhoze kuwathauzira Iwo, ndipo Iye amawathauzira Iwo kwa yemwe Iye afuna. Iwo sananene kuti, “Achivundi akale, pamene iwo anali kuyenda pa dziko lapansi mu nthawi zakale ndi njira zosiyana.” “Mulungu, mu nthawi zakale ndi njira zosiyana ankadziululira Yekha kwa aneneri Ake.” Mukuona?

⁹³ Ndipo, zindikirani, “Kwa yemwe Iye afuna amamuwululira Izo.” Ndipo Iye anazikonza izo chotero kuti Iye akhoza kudzubisa Yekha mu Malemba, kwa wazumulungu wophunziritsa yemwe alipo. O, mai! Iye akhoza kungodzibisa Yekha, atakhala apo pomwe mu Malemba, ndipo inu mukhoza kuyang’ana utali wa tsiku lonse ndipo osakhoza kuziwona izo; kuyang’ana mwa nthawi ya moyo, ndipo osaziwona konse izo. Iye akhoza kungodzibisa Yekha, atakhala pamenepo.

⁹⁴ Tsopano, chonde, kulikonse, mulole izo zilowerere mkati. Kuti, Mulungu, mu Mawu, akhoza kudzubisa Yekha chotero mu Mawu, kuti palibe wazumulungu kapena sukulu mu dziko ingakhoze konse kumupeza Iye, ndipo komabe Iye atangokhala pomwepo.

Inu mukuti, “Ndi kulondola uko, M’bale Branham?”

Nanga bwanji Afarisi ndi Asaduki? Nanga bwanji mu m’badwo uliwonse? Iye wazichita izo. Zedi. Iye anachita chotero mu m’badwo uliwonse. Tsopano ife tikanakhoza kuzifufuza izo. Tiyeni tiganize za masiku a Nowa; m’badwo wophunzira, wanzeru, momwe Iye anadzibisira Yekha mu Mawu Ake olonjezedwa. Mu masiku a Mose, momwe Iye anadzibisira Yekha. Mu masiku a Eliya, momwe Iye anadzibisira Yekha. Mu masiku a Yesu, momwe Iye anadzibisira Yekha. “Iye anali mu dziko, ndipo dziko linapangidwa ndi Iye, ndipo dziko silinamudziwe Iye ayi. Iye anadza kwa Ake Omwe; Ake Omwe sanamulandire Iye ayi.” Mukuona?

⁹⁵ Iye amadzibisa Yekha kwa ophunziritsa, munthu wanzeru yemwe alipo mu dziko. Inu mukuti, “Chabwino, uyu ndi Dr.

Bambo Woyera *Wakuti-ndi-wakuti*.” Ine sindikusamala yemwe iye ali, Mulungu amadzibisa Yekha kwa iye; ndipo amaziulula izo kwa makanda amene angati aphunzire, mukuona, makanda a Mulungu, mbewu yokonzedweratu.

⁹⁶ Taganizani. Mulungu Wamphamvu, atakhala mu Mawu Ake Omwe, akuchititsa khungu anzeru, anthu ophunzira a m’badwo umene ulipo uno, ndipo iwo sakuziwona izo. Iwo akuganiza kuti ndi gulu lakutentheka chabe. Tayang’anani pa Iye atayima apo akudzibisa, kwa Achipentekoste, Abapitsti, Amethodisti, Apresbateria. Akudziulula Yekha kunja komwe poyera, ndi kusonyeza mitundu yonse ya zinthu, ngakhale kuziyika izo mu mapepala, ndi zinthu monga izo, komabe iwo sakuziwona izo. O, Mulungu wathu, wamkulu bwanji, akudziulula Yekha kwa yense yemwe Iye afuna.

⁹⁷ “O,” inu mukuti, “M’bale Yonasi kapena M’bale *Wakuti-ndi-wakuti*, iye ali—iye ndi munthu wamkulu. Iye aziwona Izo.” O, ayi. Iye amaziwulula Izo kwa yemwe Iye afuna. Mukuti, “Mkazi wanga sakuziwona Izo, ndipo iye ndi mkazi Wachikhristu.” Iye amadziulula Yekha kwa omwe Iye afuna. “Chabwino, abusa anga ndi munthu wamkulu.” Uko nkulondola, koma Iye amadziulula Yekha kwa omwe Iye afuna. Tsopano, fufuzani ndi zomwe zaululidwa kale, pa zomwe zikuchitika, ndiye inu mudza . . . inu mukhoza kumvetsa ndithu.

⁹⁸ Tsopano ife tikuzindikira ndiye, izo zikupanga Ilo Bukhu la Mulungu ndipo osati bukhu la munthu. Ngati Ilo likanakhala la munthu. . . Tsopano tiyeni ife tiwone momwe Ilo likanati lidzifotokozere Lokha. Taonani momwe Ilo likuyalutsira tchimo la amuna amene analilemba Ilo, zindikirani, amuna amene—amene anakhala moyo mu tsiku Lake.

Abrahamu, mwa chitsanzo, iye amatchedwa “atate wa okhulupirika.” Zindikirani momwe kuti . . . Inu mukuganiza Abrahamu akanalemba Bukhu ili pa yekha, za mantha ake omwe? Inu mukuganiza bwanji kuti iye akanalemba kuti iye ananama kwa mfumu mmawa uja, ndipo ananena kuti uja anali mlongo wake, pamene iye anali mkazi wake? Kodi Ilo likanalemba za machitidwe ake amantha amene iye anawachita? Zedi, iye sakanachita konse izo.

⁹⁹ Nanga bwanji Yakobo mu chinyengo chake? Wonyenga wamng’ono yemwe Yakobo anali. Akanati mu—mu—munthu, Mhebri kulemba za m’bale wake wa Chihebri, yemwe mwa iye kuti Israeli yense anatchedwa, kodi iye akanayerekeza kuti alembe chinyengo cha kholo lomwe la fuko lonselo? Mwa Yakobo, munatuluka mbadwa; kuchokera mwa mbadwa munatuluka mafuko. Ndipo mwala wa maziko wa onse awo, Baibulo likumuyalutsa iye ngati wachinyengo. Ndi kulondola uko? Inu mukuganiza munthu akanalemba zimenezo? Ayi, bwana.

¹⁰⁰ Nanga bwanji munthu kulemba za mfumu yaikulu kwambiri imene iwo anayamba akhalapo nayo pa dziko lapansi, ngati mfumu yovekedwa nduwira; Davide, mu kuchita kwake chigololo? Kodi Ayuda awo akanati alembe konse za mfumu yawo yolemekezeka kwambiri kukhala wachigololo?

O, ife tiri nayo mbiriyakale, monga, “George Washington sananenepo konse bodza,” ndi zinthu monga izo. Ife timati, timaitcha iyo mbiriyakale.

Koma uyu ndi mwamuna, Baibulo limene limamutcha Davide “wachigololo,” ndipo iye anali. Mfumu ya Israeli, wachigololo yemwe anali woti adzakhale mwana. . . Yesu kuti adzakhale Mwana wa Davide. Mwalawapamutu womwe; ndipo bambo Ake, malingana ndi thupi, anali wachigololo. Ayuda sakanalemba konse Bukhu long a limenelo. Kodi munthu akanati alembe izi pa iye mwini? Ndithudi ayi.

¹⁰¹ Likanakhoza bwanji fuko lonyada lija la Israeli? Inu mukudziwa momwe iwo analiri onyada. Fuko lonyada la Israeli, anamka nalemba za kupembedza mafano kwawo komwe, analemba za kuwukira kwawo motsutsa Mulungu wawo, analemba motsutsa za uve, zinthu zanyansi zimene iwo ankachita, ndipo anazilemba izo mu bukhu? Iwo ndithudi akanazibisa izo. Iwo akanati angosonyeza zinthu zabwino. Koma, Baibulo ili, limatiuza chimene chiri cholondola ndi chimene chiri cholakwika. Ndilo, aliyense akudziwa kuti Ayuda sakanati alembe konse Bukhu long a limenelo, lokamba za kusayera kwawo komwe, ndi kupembedza mafano, ndi kulephera, ndi chirichonse chimene iwo anali nacho. Iwo sakanati alembe konse izo. O, ayi.

Ndiye, Ndani analilemba Ilo? Baibulo linati, mu Ahebri 1:1, “Mulungu, mu nthawi zakale ndi mmanenedwe osiyana ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri.” Ndiye, izo sanali aneneri, izo sizinali achivundi. “Mulungu!” Osati “aneneri mu nthawi zakale.” Koma, “Mulungu, mu nthawi zakale, mmachitidwe osiyana ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri.”

Ine ndiri nalo Lemba ndalilemba pano. Ine sindikudziwa chimene Ilo liri; ine sindingakhoze kulozera kwa Ilo. Kawirikawiri, pamene zinthu izi zimene ine ndikulozerako kwa izo, ine ndikuyang’ana pa Lemba. Ine ndikuti ndiyang’ane pa ilo miniti yokha, ngati inu muti mundikhululukire ine. Ilo ndi Timotero Wachiwiri 3:16. Ine—ine—ine ndimaganiza kuti ndikanati ndilikumbukire ilo, koma ine ndikupepesa. Ine ndingoima kwa miniti kuti ndipeze chimene ilo liri.

¹⁰² “Mulungu, mu nthawi zakale ndi mmachitidwe osiyana ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri.”

Tsopano Timoteo Wachiwiri 3, 3:16. Tiyeni tiwone zimene ilo likunena mu 3:16.

Lemba lonse (eya) ndi loperekedwa mwa kudzoza kwa (Aneneri? Ayi) . . . kudzoza kwa (Chiyani?) Mulungu, ndipo ndi lopindulitsa pa chiphunzitsa, ndi kutsutsa, ndi kukonza, ndi kulangiza mwa chilungamo:

Kuti munthu wa Mulungu akhoze kumayima mwangwiro, atakonzedwa bwino mu ntchito zonse zabwino.

¹⁰³ Chabwino, ndiye, Lemba lonse ndi lolembedwa mwa kudzoza. Yesu, pano pa dziko lapansi, ananena kuti miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu Ake sakanati. Iye anati Malemba onse ayenera kukwaniritsidwa. Kotero ndiye Bukhu siliri bukhu la zolemba za munthu. Ilo ndi Mabuku a zolemba za Mulungu.

¹⁰⁴ Tsopano, ife tikudziwa Mulungu anasankha mwa kukonzeratu Mpingo Wake, malo Ake, aneneri Ake, ndi zonse za iwo. Mwa kudziwiratu, Iye anamukonzeratu mneneri Wake. Ndipo pamene m'badwo ufika, Iye amakhala ndi mneneri Wake atafika pa nthawi yomweyo, ndipo ankamudzoza iye pamene Iye ankalemba Baibulo ndi iye. Tsopano, Mulungu analemba Baibulo kungoti pogwiritsa ntchito mneneri, chifukwa ndiyo njira Yake yochitira izo. Chotero, mukuona, iwo sali mawu. . . Chotero, mukuona, Iwo ndi Mawu a Mulungu, ndipo osati mawu a munthu.

¹⁰⁵ Mulungu ndi Munthu. Mulungu akhoza kunena. Mulungu akhoza kuyankhula. Mulungu akhoza kulemba. Iye sanasowe kuti azichita izo mwanjira imeneyo, koma ndi momwe Iye—Iye anasankha kuti azichitira izo. Iye sanasowe kuti azichita izo mwanjira imeneyo, koma ndi Iye anasankha kuti azichita izo mwanjira imeneyo. Tsopano inu mukuti, “Mulungu analemba ndi chala Chake, chala Chake Chomwe chaufumu, malamulo khumi. Chotero Mulungu akhoza kulemba, Mwiniwake, ngati Iye atafuna kutero.” Mukuona? Koma Iye—Iye anasankha kuti alembe Ilo kupyolera mwa aneneri, mwaona. Chifukwa izo zinali zikhumbo Zake, Mawu Ake, Iye anazifotokoza kupyolera mwa iwo, kuwapanga onse gawo, kapena gawo la Iye. Mukuona? Iye akanakhoza kulemba ndi chala Chake. Iye anatenganso chala Chake ndipo analemba pa makoma a Babeloni, “Inu mwayezedwa mu muyezo ndipo mwapezeka operewera.” Iye analemba ndi chala Chake Chomwe.

¹⁰⁶ Mulungu akhoza kuyankhula. Kodi inu mukukhulupirira Mulungu angakhoze kuyankhula? Iye anayankhula kwa Mose pa phiri, mu chisamba choyaka. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Inde, bwana. Iye anayankhula kwa Yohane, mwa mawonekedwe a nkhunda, (inu mukukhulupirira zimenezo?) kuti, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonedwa mwa Yemwe Ine ndikukondwera kukhalamo.” Iye anayankhula kwa iye. Iye anayankhula kwa Yesu pa Phiri la Chiwalitsiro, pamaso pa

Petro, Yakobo, ndi Yohane. Iye akhoza kuyankhula. Iye si bubu. Mulungu akhoza kuyankhula. Chotero Iye anayankhula kwa—kwa Yesu pa Phiri la Chiwalitsiro. Ndipo Iye anayankhula kwa Yesu pamaso pa unyinjira wonse wa anthu; pamene, anthu anati iko kunabingula, koma izo anali Mulungu akuyankhula kwa Yesu. Ndipo pafupi onse Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, ndi Yesu akuyankhula. Iye ndi Mulungu. Chotero, Mulungu akhoza kuyankhula.

¹⁰⁷ Anatenga zala Zake Zomwe ndipo analemba pa mchenga, tsiku lina. Iye ankayankhula, Iye ankalalikira, Iye ankanenera, ndi milomo Yake Yomwe, Mulungu anatero, pamene Iye anapangidwa thupi nakhala pakati pathu, “Mulungu anawonetseredwa mu thupi.” Ngati Iye angakhoze kulemba, kuyankhula, kodi Iye sangakhoze kuwawuza ena choti achite? Ndithudi akhoza. Iye akhoza kuyankhula kwa iwo, mu liwu laumunthu. Iye akhoza kulemba ndi kuwasonyeza iwo zoti achite. Iye anazichitapo izo.

Chotero, “Mulungu, mu nthawi zakale ndi mmanenedwe osiyana anayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri.” Ndipo Iye ananena, pa Kulemba uku, kuti, “Palibe kolemba Khamodzi kapena dontho liti lidzachoke konse mpaka Iwo atakwaniritsidwa,” ndiyeno Iwo nkuwonetseredwa; ndiye Iwo adzapita, chifukwa Iwo awonetseredwa. Iwo sangakhoze kupita apo, koma Mawu Okha basi akupangidwa thupi. *Kolemba* limatanthauza “mawu aang’ono.” *Dontho* limatanthauza “kachisonyezo kakang’ono.” Osati ngakhale kachisonyezo kamodzi, kofotokozeru kamodzi, chirichonse, chiti chidzalephere konse mu Mawu a Mulungu. Iwo sangakhoze kulephera, chifukwa Iwo ndi Mulungu, Mulungu atawonetseredwa mu mawonekedwe a thupi la umunthu. Pakuti, ndi Mulungu Mwiniwake mu mawonekedwe a kalata, mmawonekedwe a mneneri, akuwonetseredwa mu thupi.

Tsopano, ndicho chifukwa Yesu amakhoza kunena, “Iwo amene ankayankhula kwa inu, inu munkawatcha iwo ‘milungu,’ amene ankayankhula kwa inu mwa Mawu a Mulungu,” anati, “ndipo iwo anali milungu.” Aneneri amenewo pamene iwo anali atadzozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo anabweretsa ndendende Mawu a Mulungu, ndiye iwo anali milungu. Awo anali Mawu a Mulungu akuyankhula kupyolera mwa iwo. Ndipo akhoza . . .

¹⁰⁸ Iwo akanakhoza kungotanthauzira monga Mlembi akanawalolezera iwo kuti atanthauzire. Tsopano ngati inu mukufuna kuti mupeze izo, izo ndi Petro Wachiwiri 1:20 ndi 21. Chabwino. Chifukwa, izi, pamene Mulungu . . . “Alibe kutanthauzira kwa mseri.” Iye amachita kutanthauzira Kwake Kwake.

Mulungu amayankhula ndipo amawathanthauzira Iwo, Yekha, ndiye amawaululira iwo kwa yense yemwe Iye afuna, amawabisa kwa ena onsewo. Iye samasowa kuti awaululire Iwo kwa aliynse kupatula ngati Iye akufuna kutero. Ndipo Iye samati. . . Iye, Iye wachifotokoza chinthu Chake chonsecho mu Malemba, chotero chinthu chonsecho chadziwika kale; kungoti Iye wangokhala pamene akuyang'anira izo zikuchitika. Mukuona? Ayi. Akungowona Thupi kukhala likupangidwa ndi kubwerera kwa Ake, ku mapangidwe, Mkwatibwi Wake kachiwiri. Chabwino.

¹⁰⁹ Okhulupirira amakhulupirira Izo, monga Abrahamu yemwe anatcha zinthu zosiyana ndi Iwo ngati kuti panalibe.

¹¹⁰ Iwo naponso, Mawu awa, amazindikira zinsinsi za mitima, Ahebrei 4:12. "Iwo amazindikira zinsinsi za mtima."

¹¹¹ Aneneri sanali nthawizonse kumvetsa zimene iwo anali kulemba kapena zimene iwo anali kunena, kapena iwo sakanati mwanjira iliyonse azinene izo, ngati iwo akanati azimvetse Izo. Mukuona? Koma Baibulo limati, "Iwo ankasunthidwa ndi Mzimu Woyera." Ankasunthidwa! Pamene Mzimu Woyera ukusuntha iwe, iwe umasuntha. Munthu. . . "Mulungu, mu nthawi zakale ndi mmachitidwe osiyana ankayankhula kwa aneneri amene ankasunthidwa ndi Mzimu Woyera." Ndicho chifukwa, mibadwo yonse, anthu amene anali auzimu ankafunsira kwa aneneri zokhudza nthawi ndi zimene zikanati zichitike.

Mneneri-mlembi amayenera kukhala mu chiyanjano chowirikiza ndi Mlembi. Mukuona? Iye ayenera kumakhala mowirikiza mu Kukhalapo kwa Mlembi, kuti adziwe chimene Bukhu liti likhale. Mukuona? Mneneri-mlembi, iye ali ndi cholemba chokonzeka nthawi iliyonse, chiyanjano chowirikiza ndi Mlembi, yemwe anali Mulungu, kuti alembe chirichonse chimene Iye anena kuti lemba. Mukuona? Zimasonyeza mtundu wa moyo umene iye ayenera. . . moyo wolekanitsidwa kwa abale ake onse.

¹¹² Tsopano, ndicho chifukwa mneneri anali ndi malingaliro ake atakhazikitsidwa mowirikiza pa chimene Mulungu an anena; osati chimene anthu ankaganiza, chimene m'badwo unkaganiza, chimene mpingo unkaganiza, chimene ufumu unkaganiza. Chimene Mulungu anaganiza! Iye ankangofokoza maganizo a Mulungu kwa Mawu, chifukwa mawu ndi ganizo pamene ilo lafotokozedwa. Inu mwamvetsa izo tsopano? Mawu ndi ganizo litafotokozedwa, chotero mneneri anali kuyembekezera maganizo a Mulungu. Ndipo pamene Mulungu awulula maganizo Ake kwa iye, iye amawafotokoza iwo mu Mawu, "PAKUTI ATERO AMBUYE." Mukuona, osati "Pakuti nditero ine, mneneri." "PAKUTI ATERO AMBUYE!" Mukuona? Chabwino.

113 Ndicho chifukwa iwo ankanyoza maufumu ndi mibadwo ya mpingo, chimene, kuti achite chotero mu masiku awo, chinali chilango cha imfa. Iwe ungayende kupita pamaso pa mfumu ndi kumuwuzwa iye, “PAKUTI ATERO AMBUYE, *zakuti-ndi-zakuti* zikachitika,” iwe ukanakhoza kupangitsa mutu wako kudulidwapo. Mpingo ungakuike iwe ku imfa pakali pano chifukwa chochita izo. Koma aneneri awa anali olimbamtima. Chifukwa? Iwo ankasunthidwa ndi Mzimu Woyera, mukuona, ndipo, iwo, ndicho chifukwa amakhala olimbamtima. Ndipo iwo analemba—Mawu osalephera a Mulungu.

114 Analipo ochuluka amene ankayesera kuti awasanzire aneneri amenewo, monga ansembe, kapena ena otero. Ndipo kodi iwo ankachita chiyani? Kungosokoneza, ndizo zonse. Iwo sakanakhoza kuzichita izo.

Chifukwa, Mulungu anali atamusankha munthu wa m’badwowo, ndipo atasankha Uthenga, ndipo ngakhale khalidwe la munthu ndi chimene chikanati chidzadutse mu m’badwo umenewo, chimene Iye ati adzaika pa iwo, momwe Iye akanachitira. Ndi chikhalidwe cha munthu ameneyo, Iye amakhoza kuchititsa khungu maso a enawo. Mawu amene munthu ameneyo akanati anene, momwe iye ankachitira, zikanakhoza kuchititsa khungu enawo, ndi kutsegula maso a ena. Mukuona? Iye ankamuveka munthuyo ndi mtundu wa chovala chimene iye anali; chikhalidwe, chokhumba, ndi chirichonse basi mwanjira yomweyo iye ankayenera kuti adzakhale, wosankhidwira mwangwiro basi kwa anthu enaake amenewo amene Iye akanati adzawayitanire ku m’badwo winawake umenewo.

Pamene, enawo amaima ndi kuyang’ana pa iye, ndi kuti, “Chabwino, ine sindingakhoze. Apo . . . ine—ine sindikukhoza kuwona.” Iwo anali atachititsidwa khungu.

115 Yesu anadza mwanjira yomweyo, atavekedwa, Mulungu wachisavundi atavekedwa mu thupi la umunthu. Ndipo chifukwa Iye anabadwira modyetsera msipu, mu khola lodzaza ndowe, wopanda malo oti agonekepo mutu Wake; wobadwa, mwakuganiza, ali ndi dzina lawapathengo litakwewerekedwa pa Iye. Mukuona? Zinthu zonse izi zimene Iye anali, ndi momwe Iye anakulira, mwana wa ampalamatabwa, momwe Iye anali wosaphunzitsidwa.

Mochuluka kapena mochepa, mu dziko, nzeru za dziko lino, Iye analibe kanthu kochita ndi izo. Analibe chirichonse cha chitukuko cha dziko lino, maphunziro, kapena chirichonse. Iye analibe chinthu chimodzi choti achite ndi izo. Chifukwa? Iye ndi Mulungu. Izo zikanasokonezana. Ngati Iye akanayesera kuti apite ku seminare kwinakwake ndi kukaphunzirako chinachake chimene mipingo ya dziko iyi inali kuchita, chimene mu . . . Bwanji, izo sizikanati nkomwe . . . bwanji, izo sizikanati

nkomwe...sizikanati zigwirizane nkomwe ndi kumvetsa Kwake, chifukwa Iye anali Mulungu.

Chotero, maphunziro, kuphunzira, maseminare, ndi zinthu, ziri mwamtheradi zosiyana ndi chifuniro cha Mulungu. Kachitidwe konse ka za maphunziro ndi kosiyana ndi Mulungu. Chirichonse chimaphunzitsa motalikira ndi Mulungu, nthawi zonse. Pamene ine ndimuvva munthu akunena kuti iye ndi Dr., Ph.D., L.L.Q., izo zimangomupangitsa iye kutalikirana mochulukwa chotero kwa Mulungu, kwa ine. Mukuona? Iye wangodziphunzitsa yekha motalikira kuchulukwa chotero kuchokera ku chimene iye anaitanidwira kwenikweni kuti achite. Ndiko kulondola.

Zindikirani momwe tsopano iwo anali kusunthidwa ndi Mzimu Woyera.

¹¹⁶ Tsopano, izo sizikutanthauza kuti munthu wophunzira sakubwera umu. Tayang'anani pa Paulo. Ine ndikulingalira panalibe munthu wophunzira mu tsiku lake kuposa Paulo, yemwe anali Saulo waku Tariso. Iye anaphunzitsidwa pansa pa Gamalieli, mmodzi wa aphunzitsi aakulu a tsikulo; wamkulu, Mhebri wosamalitsa, Mfarisi wa chipembedzo. Ndipo Paulo analeredwa pansa pa iye. Iye ankadziwa chipembedzo chonse cha Chiyuda. Koma pamene iye anabwera kwa mpingo, iye anati, "Ine sindinabwere konse kwa inu mwa maphunziro a munthu, ndi zina zotero. Chifukwa, ngati inu mukanatero, ndiye inu mukanamadala mu zimenezo. Koma ine ndikubwera kwa inu mu mphamvu ndi mawonetseredwe a Mzimu Woyera, kuti chikhulupiriro chanu chikanati chikhale mwa Mulungu." Ndi inu apo. Mukuona? Ndiko kulondola.

¹¹⁷ Ambiri anayesera kuti awatsanzire anthu awa, koma iwo anangosokoneza chinthu chonsecho basi monga iwo akuchitira lero. Panali mmodzi yemwe anadzutsidwa isanafike nthawi ya Yesu, anatsogolera anthu mazana anai mosochera. Ndipo inu mukudziwa momwe Malemba amawerengeka pokhudza zinthu izi, kuyesera kuzichita izo nthawi isanafike. Ndipo ena a iwo anayesera kuti amutsanzire Iye, ndipo iwo onse anali *ichi, icho*, kapena chimodzi *chinacho*. Ndipo Iye anati, "Mu masiku otsiriza, momwe iwo akanati adzutse Akhristu abodza, mu masiku otsiriza, ndi aneneri abodza, ndi kusonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa." Ife tiri nazo zonse izo. Mukuona? Koma izo sizimachita kutali ndi chenichenicho. Izo zimangopangitsa Iwo kuwala mwabwinoko, chifukwa ife tiri naye Khristu weniweni, osati wabodzayo.

¹¹⁸ Tsopano, tsopano, ife tikuzindikira ndiye kuti Mulungu amatumiza aneneri Ake. Iyo inali njira imene Iye anali nayo ya kubweretsa Mawu Ake kwa anthu, kupyolera mu milomo ya aneneri Ake.

Ndipo zindikirani, inu mukudziwa, Mose anati, ngati inu mukufuna kuti mukawerenge izo mu Eksodo mutu wa 4, ndi ndime ya 10 ndi ya 12. Mose anati Mulungu anayankhula kwa iye. Mulungu anayankhula kwa munthu, mulomo kwa khutu. Ndipo iye anati, “Ndine wochedwa kuyankhula,” Mose anati. “Ine, ine sindiri wokwanira. Ine—ine sindingakhoze kupita.”

¹¹⁹ Iye anati, “Ndani anamupanga munthu kuti aziyankhula, kapena Ndani anamupanga iye wosayankhula? Ndani anamupanga iye kuti azipenya, kapena Ndani anamupanga iye kuti azimva? Kodi si Ine, Ambuye?” Anati, “Ine ndikakhala ndi kamwa yako.” Mukuona? Chotero . . .

¹²⁰ Ndipo Yeremia anati, ngati inu mukufuna kuti mukawerenge izo mu Yeremia 1:6. Yeremia ananena kuti, “Mulungu anaika mawu mkamwa mwanga.” Mukuona? Iye—Iye anayankhula, mulomo ndi khutu, ndi mneneri mmodzi; ndipo ankayankhula kupyolera mwa mneneri winayo, iye analibe chodziletsera nkomwe, ndipo ankayankhula kupyolera mu milomo yake.

¹²¹ Iye ali nayo njira yowafikitsira Mawu Ake kwina, inu mukudziwa. Inde, bwana. Chotero inu mukuona Baibulo ndi Mawu a Mulungu, osati mawu a munthu.

Mose anati, “Mulungu anayankhula kwa ine ndi liwu, ndipo ine ndinamumva Iye. Ine ndinalemba zimene Iye ananena.”

¹²² Yeremia anati, “Ine sindinkakhoza kuyankhula nkomwe. Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, milomo yanga inali ikuyankhula, ndipo—ndipo—ndipo ine ndinali kuzilemba.” Mulungu anayankhula kupyolera mu milomo yake, ndipo izo zinafika pochitika.

Daniele, Yesaya, ndi ena otero, aneneri onse awo anali pafupi ofanana basi.

¹²³ Inu mukudziwa, mu Chipangano Chakale chokha, ndi zoposa nthawi zikwi ziwiri zimene aneneri amenewo anati PAKUTI ATERO AMBUYE. Tsopano, ngati munthu ati PAKUTI ATERO AMBUYE, si munthuyo akuyankhula. Ngati iye akanati akhale, iye sakanati akhale mneneri, iye akanati akhale wachinyengo, mwaona, chifukwa izo sizikanati (nkomwe) zifike pochitika; mwayi umodzi mwa nthawi zikwi mazana khumi, mwaona, iwo akhoza kupeka izo. Koma ngati izo ziri PAKUTI ATERO AMBUYE, Ambuye Mulungu wanena izo.

Ngati ine ndikanati ndinene, “Pakuti atero Orman Neville”; m’bale wanga kuti, “Pakuti atero Bambo Mann”; ine nkuti, “Pakuti atero M’bale Vayle,” cha kuno, kapena ena a abale awa, aliyense wa inu; ine ndikuyankhula zimene inu munanena. Ngati ine ndiri woota, ine ndikungonena zimene inu munanena.

Ndipo anthu awa, pokhala aneneri, amati, “Si ine ayi. Ine ndiribe kanthu kochita ndi izo, koma ndi PAKUTI ATERO

AMBUYE.” Chotero Baibulo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE mwa aneneri.

¹²⁴ Zindikirani, iwo ankatenga Mzimu wa Khristu pa iwoeni, ndipo ankawoneratu zochitika zimene zikanati zidzachitike. Kunena za kuwoneratu! Iwo ankanena zimene zikanati zidzachitike uko kupyola mu mibadwo, pamene iwo anakhala, ataima, atagona, akuyenda ndi Mzimu wa Khristu pa iwo, mochuluka mwakuti iwo ankachita ngati Khristu. Ndipo owerenga akanakhoza kumawerenga izo ndi kumaganiza kuti aneneri ankayankhula za iwoeni.

Inu mukumukumbukira mdindo pamene iye anali akuwerenga Yesaya 53:1, za momwe, kuti, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa?” Mdindo ananena kwa Filipino, “Kodi mneneri akukamba za ndani, iyemwini kapena munthu wina wake?” Mukuona, mneneri ankayankhula ngati kuti izo anali iyemwini.

¹²⁵ Tayang’anani pa Davide akulira mu Mzimu, “Mulungu wanga, Mulungu wanga, chifukwa chiyani Inu mwandisiya ine? Mafupa anga, iwo akusuzumira pa ine, pa ine,” Davide. “Iwo analasa mapazi anga ndi manja anga,” Davide. “Iwo analasa mapazi anga ndi manja anga. Koma Inu simudzawusiya moyo wanga ku gehena, ngakhale kuti Inu mungadzalole woyera Wanu kuti awone chivundi,” ngati kuti Davide anali kuyankhula za iyemwini kukhala woyera. Uyo anali Mwana wa Davide, Mbewu yophuka ija, yauzimu ikubwera mmusimo kupyolera pamenepo. Ngakhale Davide mwiniwake anali chisoso, koma mkati mmenemo munali njere ya Tirigu. Inu mukumvetsa izo?

Chotero, Baibulo lonse, Ilo si mawu a munthu, ngakhale kuti Ilo linalembedwa ndi munthu, kubweretsedwa ndi munthu, kapena ngakhale kuti Ilo lingakhoze—kuwululidwa ndi munthu. Ndi Mawu a Mulungu akuwululidwa ndi Mulungu Mwiniwake, Wotanthauzira Zake Zomwe, Khristu kudziulula Yekha mu Mawu Ake Omwe.

¹²⁶ Tayang’anani pa Khristu ataima kumbuyo uku mwa Davide. Davide sankakhoza konse kuganiza tsopano. Malingaliro Ake anali atamuchokera iye, monga izo zinali. Ndipo Iye anali atapachikidwa pa mtanda, monga inu mukuwonerera chosema apa; atapachikidwa pa mtanda, akulira, “Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, chifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine? Mafupa Anga onse, iwo akuwonekera pa Ine. Iwo alasa manja Anga ndi mapazi Anga. Iwo akantha mbali Yanga.” Mukuona? “Nchifukwa chiyani Inu mwanditalikira Ine? Zimbalangondo zonse za ku Bashani zandizungulira ine. Iwo akugwedeza mitu yawo, ndi kumati, ‘Iye anadalira mwa Mulungu, kuti

Iye akanamuwombola Iye; tsopano tiyeni tiwone ngati Iye ati amuwombole Iye,” akuyankhula mawu omwewo.

Chotero, inu mukuona, pamene Mulungu anawonetseredwa pa dziko lapansi pano, Iye ananena mawu omwewo amene Davide ananena. Inu mukumvetsa izo? Chotero, inu mukuona, Si mawu a munthu; ndi Mawu a Mulungu. Ameneyo anali Mulungu mwa Davide; ameneyo sanali Davide. Iye sanali kudziwa zomwe iye anali kunena; iye anangokhala chomwecho mu Mzimu.

Ndi momwe Mose anali. Iye anali chotero mu Mzimu, anadutsa kuchokera mu malo amene iye anali kukhalamo, ndipo anaima pamenepo maso ndi maso, mu chisamba choyaka chija, akuyankhula kwa—kwa—kwa Mulungu Mwiniwake. Anati, “Vula nsapato zako. Malo amene iwe wayimapo ndi malo opatulika.”

Ine ndikulingalira pamene Mose anachoka pamenepo, iye ankaganiza, “Ndi chiyani chinachitika? Ndi chiyani chinali kuchitika? Chinali chiyani icho?”

Anati, “Pita uko mu Igupto. Ine ndipita ndi iwe.”

Iye anati, “Izo ndi zenizeni kwambiri kwa ine, ine ndiyenera ndipite.” Iye anamutenga mkazi wake ndi ana ake. . . ndi—ndi mwana wake, kani, ndi ndodo yake mu dzanja lake, ndipo anawuyamba waku Igupto, kuti akawapulumutse anthuwo. Mukuona?

¹²⁷ Mulungu akuyankhula, Mwiniwake, kupyolera mwa aneneri. Mwaona, iwo, iwo ali mwamtheradi. . . Izo sanali aneneri; izo anali Mulungu. Chifukwa, aneneri, za iwoeni, iwo sakanakhoza kunena zinthu zimenezo.

“Ndani wakhulupirira uthenga wathu?” Yesaya akuyankhula, inu mukuona. “Ndani wakhulupirira uthenga wathu? Ndi kwandani kumene mkono wa Ambuye waululidwa? Iye adzakula pamaso pathu ngati ng’ombe mu—mu khola. Ndi momwe izo, komabe, Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatuduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ife tinachiritsidwa, kutali komwe kuno mu m’badwo uwu kuno; ndipo Yesaya, mmbuyo kutali zaka mazana asanu ndi atatu asanadze Khristu. Mukuona? “Ndi mikwingwirima Yake ife tina,” zochitika kale, kale, “tinachiritsidwa.” O, mai!

Momwe, Mawu a Mulungu, aliri angwiwo kwambiri! Dalirani mwa Iwo, abale. Ndi chinthu chokha chimene chingakhoze kukupulumutsani inu.

¹²⁸ Mawu ena onse, ine sindikusamala momwe iwo aikidwa mwabwino, momwe, ndani yemwe iwo achokerako, ndi chipembedzo chiti chimene iwo akuchokerako, kapena momwe munthuyo aliri wophunzira, izo ziyenera kukhala

chosalabadiridwa mwamtheradi, chirichonse chosiyana kwa Mawu. Inu mukufuna kuti mulilembe Lemba limenelo, ndi Agalatia 1:8. Mukuona? Paulo anati, “Ngakhale ife, kapena Mngelo wochokera Kumwamba, akalalikira chinthu china chirichonse osati Ichi chimene inu mwachimva kale, musiyeni iye akhale wotembereredwa.”

Mwa kuyankhula kwina, ngati Mngelo akanati abwere kwa inu kuchokera Kumwamba, Mngelo wowala wonyezimira, ndipo akanati ayime; mnyamata, imeneyo ikanati ikhale nyambo ya tsiku lino, sichoncho izo? Mngelo wowala monyezimira akuchokera kumwamba uko ndi kuima, ndi kumanena zinthu zimene zinali zosiyana kwa Mawu; inu muziti, “Satana, pita kutali kwa ine.” Ndiko kulondola. Ngati iye ali bishopu, ngati iye ali . . . chirichonse chimene iye ali, inu musati konse mumukhulupirire iye ngati iye sali kuyankhula ndendende ndi Baibulo limenelo, Mawu ndi Mawu. Mupenyeni iye, iye akunyamulani inu ndi Baibulo tsopano. Iye akutengerani inu ku malo ena, ndiyeno nkukoloweka izo apo pomwe. Pamene inu muwona Baibulo likunena chinthu chimodzi, ndipo iye akuchilambalala icho, mupenyeni iye apo pomwe.

Mukuona, ndi momwe iye anamchitira Eva. Iye anabwera uko komwe ndipo ananena chirichonse ndendende basi. “Chabwino, Mulungu ananena *izi*. Ndiko kulondola, Eva. Amen. Ife tikukhulupirira izo, limodzi.”

“Chabwino, Mulungu ananena *izi*.”

“Amen. Ife tikukhulupirira izo, limodzi.”

“Mulungu ananena *izi*.”

“Ife tikukhulupirira izo, zedi.”

“Chabwino, koma Mulungu anati ife tidzafa.”

¹²⁹ “Chabwino, tsopano, inu mukudziwa Iye ndi Mulungu wabwino.” Iye sananene kuti Iye sakanati atero, inu mukudziwa. “Koma ndithudi . . .” O, ine! Ndi uyo pamenepo.

Ndipo ngati iye anali wachinyengo monga choncho, ndipo Baibulo limati, “Mu masiku otsiriza iye akanati adzanyenge Osankhidwa ngati kukanakhala kotheka,” kodi ife tikuyenera kukhala tiri pati lero, abwenzi? Tsopano, maphunzira aang’ono awa a Sande sukulu, ayenera kuti azichitidwa mwatcheru kwambiri, inu mukudziwa, kwa mitima yathu, kuti tiwone . . . Ife tiyenera kumamvetsera mwatcheru kwenikweni ndi kuwona momwe chinthu icho chiriri chonyenga.

¹³⁰ Zindikirani, ife sitingakhoze, ife sitiyanera ayi, kumamvetsera kwa mawu a munthu wina aliyense. Ife sitikusamala wanzeru bwanji, ndi wophunzira bwanji. Baibulo, mu Miyambo, limati, “Ife tiyenera kuponyera pansi zolingalira.” Mukuona? Tsopano, pano mu chigawo chachiwiri ichi . . .

Chigawo choyamba ndi zokhudzira zanu za kupenya, kulawa, kumverera, kununkhiza, ndi kumva. Izo ziri mu thupi lanu lakunja.

Mu thupi lamkati, limene liri mzimu, muli kulingalira ndi ganizo, ndi zina zotero. Ife tiyenera kuponyera pansi zonse izo. Sitingakhoze kulingalira, kuti, “Tsopano dikirani, ngati Mulungu ali Mulungu wabwino...” Ndipo ife timawuzidwa zochuluka chotero lero kuti Iye ali. “Ngati Iye ali Mulungu wabwino, ndiye ngati ine ndikhala wodzipereka, ngakhale ine sindingakhoze kuwona izo mu Baibulo ilo kuti ndi zolondola, ngakhale ine ndingakhale wodzipereka, ine ndidzakhala wopulumutsidwa.” Inu mudzakhala otaika. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

¹³¹ “Ngati ine ndizipita ku mpingo ndi kumangochita zinthu zimene ine ndikukhulupirira kuti ndi zolondola, ndi kuyesera kugwiritsa ku chimene ine ndikuganiza chiri cholondola, chabwino, ine...” Inu muli otaikabe.

“Pali njira imene imawoneka yolondola kwa munthu, koma mathero ake ali njira ya imfa.” Mukuona? Inu simuti mupulumutsidwe; inu mudzakhala mutataika. Mukuona? Mukuona? Izo ziyenera kukhala Munthu wolamulira wamkatiyo.

¹³² “Chabwino, ine ndinayankhula mu malirime, M’bale Branham. Chabwino, kodi inu simumakhulupirira mu kuyankhula mu malirime, M’bale Branham?” Mwamtheradi. “Chabwino, ine ndinafuula; kodi inu simumakhulupirira zimenezo?” Inde, bwana. “Ine ndimakhala moyo wabwino wa Chikhristu. Kodi inu simumakhulupirira mu izo?” Inde, bwana. Koma apobe izo sizikutanthauza inu munapulumutsidwa. Ndinu munthu wabwino; woyera, wamakhalidwe, wopatulika, munthu wabwino.

Chomwechonso anali ansembe aja, achipembedzo mpaka pachirikati, achipembedzo kwambiri mpaka kusokoneza pamodzi, iwo akanagendedwa mpaka kufa. Chilango cha imfa chifukwa chosewera ndi Mawu a Mulungu inali imfa.

¹³³ Ndi lomwe liri vuto kwa dziko lathu lero. Chifukwa chimene tiri nazo zinthu zambiri za tsamba-lothothoka mu dziko lapansi lero, zilango siziri zamphamvu mokwanira. Ngati munthu agwidwa akuthamanga ndi mkazi wa mwamuna wina, iwo onse akanayenera kuti atengedwere kugulu ndi kukafulidwa, kumene, pagulu, ndi kusiyidwa. Ndiko kulondola. Ngati munthu agwidwa akuchita chirichonse cholakwika, mu msewu, akuthamanga, iye ayenera kuti asapatsidwe zochepera zaka khumi; iye ali wo-... kupha mokonzekera. Mukuona? Inu mukaika zilango zonga izo pa iwo, inu muchepetsa izo.

Koma pamene mthakati wina wandale angakhoze kufika kwa mmodzi *uyu* apa ndi kumudutsitsa iye, ndi kuti, “Chabwino,

iyе anali kumwa pang’ono, iyе anali . . . sanali kutanthauza kuti achite izo.” Ndipo atapha bambo, mkazake, ndi gulu lonse la ana osalakwa, nkumulola Ricky kuti adutse nazo izo, ndizo ndale. Ndilo dziko. Ndiye mdierekezi.

¹³⁴ Mulungu anati ngati mwamuna agwidwa mu chigololo, kapena mkazi, atengereni iwo kunjа uko ndipo kawagendeni iwo mpaka kufa. Izo zimathetsa izo. Mukuona? Ngati iyе apezeka ngakhale akutola kolemera ngati nkhuни, pa tsiku la sabata, “Mutengeni iyе ndipo kamugendeni iyе.” Iwo ankakhala mwa izo apo. Ndipo tsopano, mukuona, ife tiribe mtundu wa malamulo amenewo lero.

Koma Akhristu, mpingo, umene ine ndikuyankhula nawo mmawa uno, lamulo limenelo la Mulungu liri mu mtima mwanu. Mukuona? Inu mulibe chikhumbo choti muchite izo. Ilo liri mkati umu. Inu mukufuna kuti musunge lamulo la Mulungu mwangwiro kwambiri. Ziribe kanthu chimene icho chiri, inu mukungofuna kuti mukhale basi chimene . . . Ngati—ngati Mulungu akusowa chopondera pa khomo, Iye akufuna kuti inu mukhale chopondera pa khomo chimenecho, ndinu wokondwa kwambiri basi kuti mukhale chimenecho. Ziribe kanthu chimene izo zikanati zikhale, inu mukufuna kuti mukhale chopondera pakhomo. Mukuona? Chirichonse chimene Mulungu akufuna inu kuti muchite, ndicho chimene inu mukufuna kuti muchite, chifukwa ndi Mulungu. Tsopano, ndi pamene inu mumapeza kwenikweni chikondi chanu chenicheni, choona, kwa Mulungu.

¹³⁵ Tsopano ife tikupeza ndiye, kuti, “Mngelo akanati alalikire china chirichonse,” pambali pa chimene . . . ? . . . zanedwa kale mu Baibulo, “msiyeni iyе akhale wotemberedwa.” Palibe wina angakhoze. Sungakhoze kuchita izo; Izo ziyenera kukhala ndendende basi momwe Izo zikunenera.

¹³⁶ Ndipo kachiwiri ife tikuwerenga, mu Chivumbulutso 22:18 ndi 19, “Ngati munthu aliyense ati awonjezere Mawu amodzi kwa Awa, kapena kuchotsa Mawu amodzi kwa Iwo, Mulungu adzachotsa gawo lake mu Bukhu la Moyo.” Kulondola. Mulungu adzachotsa gawo lake, ngakhale iyе akhale mtumiki, chirichonse chimene iyе angati akhale, ndi mawu ake . . . dzina lake litalembedwa pa Bukhu la Moyo. Mulungu anati, “Ine ndidzangolifuta ilo apo,” ndiko kulondola, “ngati iyе awonjezera chinthu chimodzi kwa Iwo, kapena akachotsako Mawu amodzi kwa Iwo.” Ndi momwe Mulungu wosalephera wawapangira Mawu Ake. Mukuona? Inu mukhoza kuwonjezera kwa mpingo, kapena kuchotsa kwa mpingo. Inu musati muwonjezere kwa Mawu amenewo, kapena kuchotsako kwa Iwo, chifukwa Mulungu adzachotsa dzina lanu pomwepo pa Bukhu la Moyo. Ndipo, ndizo, inu mwathedwa ndiye. Mukuona? Inu simungakhoze kuwonjezera kwa Iwo, kapena kutenga kuchotsa kwa Iwo. Ziri ndendende basi zimene . . .

¹³⁷ Iwo samasowa wotanthauzira, pakuti Baibulo linanena kuti Mulungu amachita kutanthauzira Kwake Komwe pa Baibulo. “Iwo ndi opanda kutanthauzira kwamseri,” anatero Petro. Chabwino.

¹³⁸ Ndipo Lemba lonse ndi loperekedwa Mwaumulungu, linakhazikitsidwa Mwaumulungu mu dongosolo, ndipo chinthu chonsecho chiri yumbulutso la Yesu Khristu. Chipangano Chatsopano ndi Chakale, pamene iwo ananeneratu za kudza kwa Iye, chimene Iye akanati adzachite pamene Iye adzafika kuno, ndi chimene Iye akanati adzachite mu m’badwo ukudza uwu. Chotero izo zimamupangitsa Iye yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mukuona?

Monga mu Ahebri uko, pamene Paulo analemba izo. Iye ndi Mulungu, “Yesu Khristu dzulo,” wa Chipangano Chakale. Iye ali “Yesu Khristu lero,” akuwonetseredwa mu thupi. “Ndipo Iye ndi Yesu Khristu kwanthawizonse,” mu Mzimu, “woti udze.” Mukuona? Mukuona? “Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

Ndipo Iye ali wamoyo nthawizonse kuti awapange Mawu Ake kukhala chimene Iwo anati Iwo akanati adzachite kwa m’badwo umenewo. Iye ali wamoyo.

¹³⁹ Iye anali wamoyo mu Chipangano Chakale, ankawonetseredwa. Ine ndikungofuna kuti ndikuloleni inu muwone chinachake chaching’ono pano, ngati inu mungakhoze kupirira nacho. Penyani, pamene Yesu anawonetseredwa mu Chipangano Chakale, monga ife timakhulupirira izo.

Tsopano, inu alaliki kunjira uko, inu muti mutsutsane nazo izi, chitani chirichonse chimene inu mukufuna, koma ine ndikuyankhula kwa anga...chimene ine ndikuganiza. Mukuona?

¹⁴⁰ Pamene Yesu anawonetseredwa mu Chipangano Chakale, mu fiofane, mwa munthu uja Melkizedeki; osati unsembe, koma Munthu, Mwamuna. Mukuona? Pakuti, Mwamuna uyu anali asanabadwe apabe, koma Iye anali mu fiofane, chotero Iye anali wopanda atate, wopanda amake. Iye anali Mulungu Mwiniwake. Iye anawonetseredwa mu mawonekedwe a Munthu, wotchedwa, “Mfumu ya Salemu, yemwe ali Mfumu ya Mtendere, ndi Mfumu ya Chilungamo.” Mukuona? Iye anali Melkizedeki. “Iye analibe ngakhale bambo kapena amake, chiyambi cha masiku kapena mapeto a moyo.” Mukuona? Iye anali Yesu mu fiofane, mwa mawonekedwe a Munthu. Kodi inu mungapite nazo izo? Chabwino.

¹⁴¹ Ndiye Iye anadzapangidwa kwenikweni munthu wathupi, ndipo anadzakhala pakati pathu, mu Umunthu wa Yesu Khristu Mwiniwake, wobadwa kwa namwali Maria. Iye anabwera mwa mawonekedwe amenewo kuti Iye akanakhoza kufa, ndipo anapita kubwerera Kumwamba.

Tsopano mu masiku otsiriza ano, Iye walonjeza kuti adziwonetsere Iyemwini mu chidzalo kachiwiri, cha thupi Lake, mu Mzimu. Mukuona? “Pakuti monga izo zinali mu masiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala ziri mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Tsopano tayang’anani pa Sodomu, momwe iye wakhallira, ndi chimene chidzachitika. Ndipo Yesu Khristu kukhala akuwonetseredwa mwa mawonekedwe a thupi, la Mpingo Wake lero, mukuona, akuchita chinthu chomwecho, ntchito yomweyo, zinthu zomwezo zimene Iye ankachita nthawi zonse, samasintha konse, Mmodzi Wamuyayayo. Mukuona? Ndipo pa dziko lapansi lero, Iye wadziwonetsera Mwiniwake mu matupi aumunthu, matupi athu aumunthu amene Iye wawaitana, ndipo wachita ndendende chinthu chomwecho Iye anachichita mu nthawi zakale, ndi mu nthawi za thupi Lake pa dziko lapansi. Ndipo akuchita chinthu chomwecho lero, chifukwa, “Mulungu mu nthawi zakale ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri, mu masiku otsiriza ano kupyolera mwa Mwana Wake, Yesu Khristu.” Mwaona, Mwana kukhala akuwululidwa mu masiku otsiriza, Mulungu kuwonetseredwa mu thupi laumunthu, chisanafike kumene chiwonongeko cha Sodomu, kutha kwa dziko la Amitundu. Inu mukuziona izo?

Pali mawonetseredwe atatu.

¹⁴² Tsopano, chinthu chotsatira kuchitika, ndi pamene izo zonse zikusonkhanitsidwa mwa Munthu mmodzi ameneyo, Yesu Khristu, Mkwatibwi ndi Thupi, pa kubwerera mwathupi kwa Ambuye Yesu. Kupanga nthawi Zake zitanu... Pamene Iye anabweretsedwa pa dziko lapansi; naphedwa, napachikidwa, nawukitsidwa. Anadziwonetsera Iyemwini mu mawonekedwe a Thupi Lake, limene liri Mkwatibwi Wake, Mkazi. Inu mwamvetsa izo? Iye ali gawo la Thupi Lake.

Ndipo mkazi ndi mwamuna angokhala apafupi limodzi kwambiri, mpaka iwo angokhala pafupi. . . Iwo ali ofanana. Iwo ayenera kukhala ali, mulimonse. Ndi awo pamenepo, mwaona, iwo ali basi kuwonetseredwa ndendende mofanana. Iye ali gawo la iye, chifukwa iye anatengedwa kuchokera kwa iye.

Ndipo Mkwatibwi lero ndi wotengedwa kuchokera ku thupi la Khristu, amene ali kuchita ndi kupanga basi ndendende monga Iye anati Iye akanati adzachite kwa tsiku lino, Mkwatibwi, Mfumukazi; Mfumu ndi Mfumukazi. Chabwino.

Ife tikufika pochedwa tsopano, chotero ife tikufuna kuti tifulumire ndi kutsirizitsa.

¹⁴³ Chabwino, Baibulo lonse liri vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu, kudzipanga Iyemwini kudziwika kwa m’badwo uliwonse. Iye anadzipanga Iyeyekha kudziwika mu masiku a Lutera, ngati maziko; mpingo, phazi, miyendo.

Monga Iye anachitira Mfumu Nebukadinezara; inu mukukumbukira momwe iye analotera maloto aja, ndipo kubwera kuchokera ku mutu kutsika? Mukuona? Tsopano Iye akubwera kuchokera ku mapazi chokwera. Mukuona? Mu ufumu wa Chibabelonia Iye anasonyeza Chipangano Chakale chonsecho, Iye anabwera kuchokera ku mutu kutsika, mpaka Iye atafika pansu mpaka Mulungu Mwiniwake kusandulika thupi pa phazi la makwerero. Tsopano kuno mu Chipangano Chatsopano, Iye akudzibweretsa kubwerera chokwera kachiwiri, ku Mutu kachiwiri, Mutu wa golide, kuti uvekedwe nduwira. Mukuona? Tapenyani. Inu mukumvetsa izi?

Mwaona, Mulungu anali pachiyambi, ndipo Iye anapitirira kubwera pansu, kupyolera mwa aneneri, ndipo mpaka pansu, mpaka Mulungu Mwiniwake anakhala waumunthu monga ife, mpaka pansu pa phazi la makwerero, mwana wobadwa mu khola; wodedwa, wokanidwa, wonyozedwa, ndi dzina loyipa, ndi chirichonse Iye anali. Ndiye Iye anayamba kukwera, mukuona, ndipo kuchokera ku mapazi Iye anayamba kumanga Mpingo, Mkwatibwi, kubwerera, kupitirira mmbuyo; ndipo tsopano kutulukira kupita mu Mwalawapamutu, kumene izo zonse zikulumikizana limodzi ndi kupanga Thupi limodzi lalikulu lowalitsidwa la Yesu Khristu.

¹⁴⁴ Mulungu ali kuwululidwa mu m'badwo uliwonse mwa Mawu Ake olonjezedwa kwa m'badwo umenewo. Tsopano tiyeni tingoyang'ana chimene ena a malonjezo Ake ali a lero, pamene ife tiri kutseka tsopano mu mawu otsiriza awa.

¹⁴⁵ Tsopano Mulungu ali kudziulula Yekha mu Kuwala kwa nthawi yamadzulo. Tiyeni tiwone tsopano. Ife tikuona . . .

¹⁴⁶ Ine ndangokhala ndi mulu wa Malemba ndawalemba apa. Monga inu mukukhoza kuwona pa tsamba ili, kuchuluka kwa Malemba amene alembedwa pamenepo. Koma, ife tangotsala ndi pafupi maminiti khumi ndi asanu kuti ikwane thwelofu. Ine ndikufuna tituluke. Ndipo ine sindinasase mawu, mmawa uno, ndikuyankhula. Nthawizina zobweretsa mpweya izi muno zimandipangitsa ine kusasa kwenikweni.

Chotero ngati M'bale Neville sali . . . Inu mulibe chirichonse cha usikuuno? [M'bale Neville ati, "Ayi."—Mkonzi.] Chabwino, chabwino, ine ndidza . . . Ngati ziri bwino, ine ndiri ndi chinachake. Ine ndinapeza paketi ya ndudu, tsiku lina, ili mu nkhalango; ndipo ine ndinapeza Uthenga kuchokera pa paketi ya ndudu imeneyo, wa usikuuno, Ambuye akalola. Mukuona?

Chotero, ine ndiri nawo Malemba awa pano. Ndipo ine sindikufuna kuti ndipite mopitirira nthawi, chotero inu mukakhoze kubwerera.

¹⁴⁷ Paketi ya ndudu, kuyankhula. Chabwino. Ine ndinali kudutsa mu nkhalango, ndipo apo panali paketi ya ndudu, ndipo

ine ndinangoyendabe motalikira. Ine ndinaganiza, “Chabwino, winawake ali patsogolo pa ine.”

Ndipo Chinachake chinati, “Tembenekira mmbuyo ndipo kaitole imeneyo.”

Ine ndinaganiza, “Ndikatole paketi ya ndudu? Osati ine.”

Chinachake chinati, “Tembenekira mmbuyo ndipo ukatole paketi ya ndudu imeneyo.”

Ndipo ine ndinapita uko, apo panali paketi yopandamo kanthu, ndipo ine ndinawona chinachake. Ine ndikuuzani inu za izo, usikuuno, Ambuye akalola. Chabwino.

¹⁴⁸ Tsopano ife tikuti tikambe za Kuwala kwamadzulo, kwa mphindi zingapo zokha. Baibulo limaneneratu kuti ikanati idzabwere nthawi, pa kutsekera komwe kwa nthawi, kuti dzuwa likanati lidzatuluke, ndipo pakanati padzakhale Kuwala kwamadzulo. Ife tonse tikudziwa zimenezo. Sichoncho ife? Ife, ife tiri. . .Ife amene tiri owudziwa Uthenga wathu lero wochokera kwa Ambuye Yesu, ife tikukhulupirira kuti pakhala pali Kuwala kwamadzulo. Ndipo Kuwala kwa madzulo uku. . .

Ndithudi, Kuwala kwakukulu kudzadza pamene Yesu Mwiniwake ati adzakhale akuwonetseredwa kuno pa dziko lapansi, kapena mmwamba mu Miyamba, akumutenga kupita naye Mkwatibwi Wake, ndiyeno Zakachikwi zidzakhazikikamo.

¹⁴⁹ Koma ife tiri nayo imodzi ya nthawi zowopsya kwambiri kuti tidutsemo, imene inayamba yakhalapo pamaso pa anthu. Ndipo ine ndiri kungoyembekezera oralo, ndipo pamene ife tidzakhoze kutenga. . .aliyense akhoza kukhala nawo mwayi pamene inu muli ndi kupuma ku ntchito ndi kukatha masiku angapo, ndipo ife tikhoza kukakhala kwinakwake kumene ine ndingakakhoze kudzakayankhula pa Miliri imeneyo ndi zinthu zimene ziti zigwe mu masiku otsiriza; ndi kuponyera pafupi masabata awiri kapena atatu limodzi, ndi kubweretsa izo limodzi, ngati Ambuye andilora ine kuti ndikhale moyo kuti ndizichite izo ndipo akadzandidzoza ine kuti ndichite chotero, kuwona momwe zinthu izo ziti zidzagwetsedwere mkati, ndi Mabingu amenewo. Ndiye inu mudzapeza zimene munthu uja ndi anthu aja akhala akuzilota, ndi zinthu zonse izi uko, izo zidzafika pochitika; mwaona, inu mudzazindikira zimene iwo anawulula, bingu lalikulu lija limene likubwerapo kuchokera—kuchokera mu mlengalenga. Tsopano, ndithudi, gulu lonse la inu, inu mukudziwa kuti ine ndikudziwa chimene izo—chimene izo zikutanthauza, inu mukuona. Ndipo, koma tiyeni tingodikira mpaka nthawiyo ifike, inu mukuwona, kuti izo zikhale, onani, tsopano, ndipo izo zidzakhala kwambiri mu nyengo.

¹⁵⁰ Tsopano, chotero ife tikuti tiwerenge zina za izi—Malemba awa mkati umu. Tsopano, mu Kuwala kwausiku kubwera, tsopano, ife tikuzindikira kuti iko kuyenera kuti kukhale Kuwala komweko kumene kunalipo mmawa.

Chifukwadi, palibe dzuwa limodzi mmawa ndi lina masana. Ndi dzuwa lomwelo. Dzuwa lomwelo limene liri masana ndilo mmawa; lomwelo mmawa monga madzulo.

Tsopano, Iwo anati, “Tsiku palokha,” tsiku pakati pa nthawi imeneyo, “lidzakhala la mtundu wonga, o, wonga chimbuwuzi, tsiku lamdima. Ilo silingakhoze kutchedwa usana kapena usiku, pakati pa izo.”

¹⁵¹ Mwaona, ndiko kupangika kwa Thupi, kuchokera ku mapazi, kubwera mmwamba. Pamene Iye anali pano pa dziko lapansi, Iye anali Mwana, Kuwala, ndiye Iye anaphedwa. Mpingo unatenga malo Ake, kenako ofera ndipo unapita kudutsa Mibadwo ya Mdimba, ndipo unayamba kumanga pa maziko kumabwera poyera. Ndiye kupenya kumachokera pati? Pamwamba pa mutu.

Mukuwaona masomphenya aja; a Nebukadinezara? Mukumuwona Iye akupita mmusi, kuchokera koyamba kwa m’badwo wa Amitundu Magazi asanakhetsedwere kwa iwo ndi kupanga chitetezero. Iwo anali opotozedwa atabweretsedwa umo. Koma zindikirani izo zinapita mmusi kumene, mmusi kumene, mmusi kumene mpaka pansu, mu chophiphiritsa, mwaona, anazibweretsa izo mmusi.

Ndiye iwo unayamba chammbuyo kumene, kubwerera mmbuyo, Mpingo unabwerera mmbuyo kuchokera kumapazi, kubwera chammwamba. Tsopano iwo uli mu nthawi ya mutu—nthawi ya mutu. Tsopano zindikirani Kuwala.

¹⁵² Inu simungakhoze kuwona ndi manja anu, komabe ndi gawo la thupi. Inu simungakhoze kuwona ndi makutu, komabe iwo akhoza kumva. Inu simungakhoze kuwona ndi mphuno, komabe izo zimanunkhiza. Inu simungakhoze—inu simungakhoze kuwona ndi milomo, ngakhale iyo imayankhula; mwaona, umenewo unali m’badwo wa Chipentekoste. Koma tsopano ziri mu nthawi ya diso, kupenya. Mukuona? Tsopano, kulibe chiwalo chimodzi chosuntha pamwamba pa maso. Ndi kulondola uko?

Chotsatira ndi luntha, chimene chiri Khristu Mwiniwake, Yemwe amalamulira Thupi lonse.

Palibe chosuntha, kuyenda pamwamba pa izo. Mukuona? Chinthu chirichonse chakhala chikusuntha. Mukuona? Kusuntha mapazi anu, kusuntha akatumba anu mu miyendo yanu, kusuntha chirichonse. Kusuntha anu... Makutu anu akhoza kusuntha, mphuno zanu, milomo yanu, ndi zina zotero. Koma mukadutsa maso anu, kulibe kanthu kamasuntha.

Ndicho chifukwa iwo amanena kuti mwamuna amakhala ndi dazi msanga, ndi chifukwa, mukuona, sikumakhala zochitika zoti zizipanga akatumba mu—mu tsitsi, khungu. Mwaona? Ndipo iwo ulibe chawofuwofu kuti iwo azifikitsa magazi mmwamba umo. Magazi sangapope kudzeramo, mwaona, sangakhoze

kupita mmwambamo ndi kukapereka magari. Ndithudi, mu—muzu wa tsitsi umakhala moyo ndi magari.

Ndipo tsopano ife tikupeza kuti gawo limenelo, inu mukuona, kulibe chirichonse mukadutsa maso.

¹⁵³ Tsopano tiyeni tipeze izo. “Kudzakhala kuli Kuwala” (pafupi pakati pa tsiku?) “pa nthawi ya madzulo!” Kodi Kuwala kumatumizidwira chiyani? Kuti inu mukhoze kuwona kumene inu muli...momwe mungati muziyendera pozungulira. Ndi kulondola uko? Kuti muziwona pamene inu muli. “Kudzala kuli Kuwala pafupi nthawi ya madzulo.”

¹⁵⁴ Tsopano, ife titenge izo tsopano ndi kuzifanizitsa izo ndi Malaki 4. Iye analonjeza kuti kudzakhala kuli Kuwala kutabwera kachiwiri mu nthawi yamadzulo, mwaona, “Pakuti, taonani, Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri, ndipo iye adzabwezeretsa—ana kubwerera kwa atate, ndi atate kwa ana,” (ndi kulondola uko?) “kuti Ine ndingabwere ndi kudzakantha dziko lapansi ndi themberero.”

¹⁵⁵ Tsopano tiyeni titenge Yohane kapena...Luka Woyera 17:30, ndipo penyani zimene Yesu analosera kumeneko, kunena kuti, “Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, izo zidzakhala zofanana...”

Tsopano kumbukirani, zindikirani, izi ziri pa nthawi imene Mwana wa munthu ati adzakhale atawululidwa; kuwululidwa kwa Mwana wa munthu. Tsopano, Mwana wa munthu anali makamaka atawululidwa mwakungoyankhula, kwa mphindi zochepa zokha uko, Sodomu asanawotchedwe kumene. Tsopano, Mwamuna ameneyo anali Elohim. Ameneyo anali Mulungu; ndipo Yesu ndi Mulungu. Ndipo Mulungu anawululidwa mwakungoyankhula pomwepo kwa mphindi zingapo, kuti ayankhule kwa Abrahamu, mu kufufuza kwa chiweruzo. Mochepa pang’ono pokha, Mwana wa munthu anawululidwa; Mwana wa munthu, Elohim. Kodi inu mukuziona izo, mpingo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Mwana wa munthu, Elohim, anawululidwa kwa maminiti angapo okha. Pakuti, mmawa wotsatira womwe iwo unawotchedwa, (liti?) dzuwa lisanati litulukire kachiwiri.

Chotero sipangakhoze kukhala bungwe linanso latsalira, ngakhale kuti pangakhoze kukhala kupitiriza kulikonse koposa zimene ziri kuchitika pakali pano, pakuti ilo lidzawotchedwa tsiku lisanatulukire kachiwiri. Chitsitsimutso chatha, kudutsa fukoli. Sikuti kukhala zitsitsimutso zinanso, zitsitsimutso zazikulu zosesa; fuko lino silinalandire konse izo. Inu mukhoza kukhala nawo osonkhana mwaluntha. Koma, ine ndikutanthauza, chitsitsimutso Chauzimu, ife taziwona zonse izo. Ine ndikuyembekeza inu mukuzigwira izo. Ine ndikunena izo mwa njira yotero—kuti ine ndikuyembekeza kuti inu mukuzimva izo. Mwaona? Izo zatha.

Mtumiki wabwino ananena, kanthawi kapitako, anati, “M’bale Branham, ngati ine ndikanakhoza kungokhala nacho chisangalalo cha Ambuye mu mtima mwanga!”

Ine ndinati, “Mwananga, chitsitsimutso chatha.” Mukuona?

¹⁵⁶ Tsopano zochititsa bata zayikidwa mu ngalawa. Mafunde aakulu owopsya ali kunja kuno patsogolo pathu; koma ife tikudziwa, kungodutsa funde ilo uko, ife tiri kuyandikira gombe. Mukuona? Ife tiri kuyandikira gombe. Ingokhalani bata. Ingokhalani mu Mawu. Khalani ndi Mulungu. Ziribe kanthu momwe inu mukumverera, chimene china chirichonse; ingokhalani limodzi ndi Mawu. Muwalole—muwalole—muwalole iwo akhale mwabata, pamene inu mukuona mitambo yonse yayikulu kwambiri iyi pozungulira ife, ndi mikuntho ikudza, ndi mabomba a atomiki, ndi china chirichonse chimene iwo akuchikamba. Koma zodzetsabata zathu ziri basi molunjika mu Mawu. Mulungu anati izo zikanati zidzakhale ziri kuno; ife tidutsa chirichonse cha izo. Eya, ife tipita kumene pamwamba pa izo. Inde, indedi! Iwo, iwo sangakhoze kutititimiritsa ife. Iwo sangakhoze kutimiza ife. Inu mukatiyika ife mmanda; ife tidzatulukamo kachiwiri. Ndizo basi zonse ziripo kwa izo. Palibe njira mu dziko yousungira iwo panso apo. Ife tidutsa chirichonse cha izo, chifukwa Mtsogoleri wathu Wamkulu akuyitana ku mbali inayo.

Ife tazikika mwa Yesu, mikuntho ya moyo ine ndiipirira;

Ife ndazikika mwa Yesu, ine sindikuwopa mphepo ina kapena funde;

¹⁵⁷ Chirichonse chimene icho chikanati chikhale, chisiyeni icho chibwere. Chimene chingati, chimene chingadzati, sizipanga kusiyana kulikonse. Ife tazikika apo pomwe mwa Yesu. Ngati ine ndikhala moyo, ine ndikhalira moyo kwa ulemerero wa Mulungu. Ngati ine ndifa, ine ndifa kwa ulemerero wa Mulungu. Ine—ine—ine ndikungofuna basi. . . Izo ziri kwa ulemerero wa Mulungu, ndi chimene ine ndikufuna kuti ndichite. Pamene izo zonse zatha, ine sindikufuna kukhala motalika kenanso. Ine ndikufuna kuti ndipite kumene. . . ku mphoto yanga imene Iye anandigulira ine; osati imene ine ndinapindula, koma imene Iye anandigulira ine, imene Iye anapereka kwa ine mwa chisomo Chake.

¹⁵⁸ Chotero ife tikuwona Kuwala kwamadzulo pano. Ndipo icho chimachita chiyani kuti tikhale nako Kuwala, ngati inu mulibe maso aliwonse kuti muziwonera momwe mungamayendere ponsepo mu Iko? Kodi Kuwala kwamadzulo ndi chiyani? Kuwala kukubwera powoneka, kuti kuwulule chinachake. Ndi kulondola uko? Ngati pali chinachake *pano*, inu mukumverera ndipo inu simuli kumvetsa chimene icho chiri, mu mdima, ndiye yatsani kuwala. Iko nkoti kuwulule! Kodi Malaki 4 ndi woti achite chiani? Mukuona? Kuchita chinthu chomwecho. Kodi

kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri nkoti kuchitenji, kumene zipembedzo zonse izi zikuzandima kuzungulira mu izi...?.. Nkoti kuulule, kutulutsira kunja. Ngati inu mulibe maso aliwonse, ndiye ndi cha ntchito yanji kuulula? Payenera kukhala maso, choyamba, kuti uwone. Ndi kulondola uko? Kuti kuulule Malaki 4, kuulula Luka Woyera 17:30, Yohane Woyera 14:12, ndiponso Yohane 15:24, 16:13. Ndi kutinso aulule Chivumbulutso 10:1 mpaka 7, kutsegula kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, ndi Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri; kuti atsegule, kuti aulule, pamene Kuwala kwamadzulo kubwera. Tsopano ngati munthu. . .

¹⁵⁹ Mu M’badwo wa Laodikaya, anthu anali (chiyani?) “amaliseche.” Kodi iwo ali? “Akhungu.” Kodi Kuwala kumachita ubwino wanji kwa munthu wakhungu? Ngati wakhungu atsogolera wakhungu, kodi iwo onse sagwera mu dzenje? “Amaliseche, akhungu, ndipo sakuzidziwa izo.” Ngakhale mphamvu za malingaliro zawo zapita, kulingalira kwawo kwauzimu kwaubongo, kumvetsa kwauzimu. Mukuona?

“Ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu; okuswa chigwirizano, onenera zabodza, osadzigwira, ndi onyoza iwo amene ali abwino; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yakeyo.” Mphamvu ya vumbulutso; iwo sakhulupirira nkomwe mu izo. Mukuona? Iwo samakhulupirira mu zinthu zotero monga aneneri. Ndipo chotero iwo samakhulupirira mu izo. Iwo amakhulupirira kuti—kuti Malaki 4 adzakhala mpingo winawake kapena bungwe linalake.

Pamene iye anabwera nthawi yoyamba, iye anali mwamuna. Pamene iye anabwera nthawi yachiwiri, ali ndi magawo awiri, iye anali mwamuna. Pamene iye anabwera mu mawonekedwe a Yohane M’batizi, iye anali mwamuna. Mukuona?

Mu masiku otsiriza, pamene Kuwala kwamadzulo kudzayamba kuwala, maso adzakhala atatseguka ndipo inu mudzawona kumene inu mukupita. Ndiye Thupi lapangidwa kale, likuyima pa mapazi ake, litatenga mayendedwe, kusunthidwa ndi Mzimu Woyera. Chiyani? Mmodzi yemwe uja yemwe anasuntha pa aneneri amene analemba Baibulo, Mzimu Woyera yemweyo akusuntha mu Thupi lodzazidwa ndi Mzimu Woyera, anasuntha mwa Mzimu Woyera, kuchokera ku bungwe lililonse, mtundu uliwonse, lirime, ndi anthu.

¹⁶⁰ Dona wamng’ono kuno, iye si wa bungwe lino, kapena bungwe lino. . . kukhala wa gulu lino. Iye amachokera kwina kwakenso, ndipo iye anabwera muno mmawa uno, anali ndi chithunzi pamenepo. Iye anali. . . anachipereka icho kwa mwana wanga, yemwe anadabwitsidwa kwambiri. Ine sindikudziwa ngati iye anayamba wamvapo za Izi kapena ayi. Ine sindikudziwa. Iye anali ndi chithunzi cha Mngelo uyu wa

Ambuye yemwe anali pa Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zotsegulidwa, kunja uko, pamene izo zinatero. Anati, anayang'ana mmbuyo kupyolera pamenepo, ndipo iye anachiwona icho chitaima mu mlengalenga, mu loto. Ndipo iye anayang'ana mmbuyo kupyolera pamenepo ndipo anachiwona icho, anamuwona winawake mu zoyera, akuguba cha mtsogolo; ndipo kumbuyo kwa izo, anati izo zimawoneka . . . Anati, "M'bale Branham, uyo munali inu." Ndipo anati, "Munaguba kulowa mmenemo," anati, "kumbuyo kwa inu, kunali anthu a mitundu yosiyana, atanyamula mbendera; Georgia, Alabama, malo amitundu yonse yosiyana, akuguba chamtsogolo," akubwera mmwamba kupita mu umutu komwe Khristu anali kuwululidwira mu masomphenya. O, alaluya!

¹⁶¹ Ife tiri mu masiku otsiriza, ndi maora otsiriza a masiku. Kodi inu mukumuwona Iye tsopano mu Mawu Ake, ndi Mawu Ake onse akuchita kuwonetseredwa pomwe pano patsogolo pathu? O, Mpingo wa Mulungu wamoyo, imani pa mapazi anu, mukhulupirireni Iye ndi zonse zimene ziri mwa inu. Gwiritsani kwa Gudumu laling'ono ilo mkati mwa gudumu, mulole Ilo likhazikitse kusuntha kulikonse ndi kuyenda kulikonse kumene inu mupanga. Lingaliro lirilonse limene inu muli nalo, mulole ilo likhale likulamuliridwa ndi Nsanja iyi mkati mwa inu. Chifukwa, Mulungu akukhala kumene mu Mawu Ake a ora lino, mu Kuwala kwamadzulo, akusonyeza Kuwala.

¹⁶² Khungu la mleme! Inu mukhoza kuyatsa kuwala, ndipo mleme—mleme ukhoza kukhala wakhungu kwambiri iwo sungakhoze kuwuluka. Kazizi wozuma, zonse izo zoyenda usiku, ndi zinthu monga izo, mphemvu ndi zinthu, sizimakhoza kuwona mu kuwala kwa tsiku. Izo sizimadziwa chimene icho chonse chiri. Izo sizingakhoze kupenya.

Ndipo Kuwala kwamadzulo kwayatsidwa. Fanizo lirilonse, kulikonse kumene ife tipitako, ku chirengedwe, ku Baibulo, ku—zosedwa zimene Melk- . . . chimene Daniele anachiwona, ndi—ndi mfumu ya tsiku limenelo, onse a iwo anaziwona; ndi zinthu zonse izi, aliyense, mawonekedwe aliwonse, kusuntha kulikonse, malo aliwonse mu Thupi, mwapamalo zikutisonyeza ife ora lomwe limene ife tiri kukhalamo. Osati kusuntha kwina kumene kungabwere pamwamba pa iko.

Panali kusuntha kwa dzanja; chikondi, Wesile. Panali kusuntha, kwa maziko; Lutera. Chikondi, panalibe konse chokulapo; iko kunkatchedwa kusuntha kwa Wesile. Iwo anatomiza amishonare ku dziko lonse. Kumodzi kwa kusuntha kwakukulu kumene kunapangidwa, mu m'badwo usanadze uwo.

Ndiye panadza m'badwo wa Chipentekoste; kenako kunadza zala zosiyana ndi zinthu, m'badwo wa Chipentekoste, wa malirime, ndi mphuno, ndi zina zotero.

Tsopano izo ziri mu maso. Maso mungawafunire ubwino wanji, kapena kufuna kuwala, ngati maso awo akanati asakhale pamenepo kuti aziwona? Payenera kukhala pali maso, choyamba, kuti muziwona. Ndiyeno pamene iwo anabwera, Iye anatsogola Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri ndipo anawulula Kuwala kwamadzulo, kutenga zinsinsi zonse zimene zakhala zitabisidwa mmusimo kudutsa mibadwo ya mpingo iyi, ndipo tsopano kuwulula izo monga Iye analonjeza kuti achite izo mu Chivumbulutso 10:1 mpaka 7. Pano ife tiri lero titakhala mkati mwa Mawu, ndipo Mawu kukhala akuwululidwa kwa ife ndi Yesu Khristu. Ndiye, *Awa* ndi Mawu a Mulungu.

¹⁶³ Ndipo pokhala omumvera Ake, ife tiyenera kumayenda pafupi ndi Mlembi, kuti tiwamvetse Iwo, kuti Iwo awululidwe. “O Ambuye, Inu mungakhale ndi chiani kwa ine, kuti ndichite? Ngati ine ndiyenera kuti ndizipita ku minda kuti ndikalalikire Uthenga, kapena kodi ine ndizikhala kunyumba? Ziribe kanthu chimene icho chiri, ngati ine ndiyenera kuti ndikhale mkazi wabwino wapanyumba, ngati ine ndiyenera kukhala mayi wabwino, ngati ine ndiyenera kumachita *ichi, icho*, kapena *chimizake*? Chirichonse chimene icho chiri, ngati ine ndiyenera kuti ndikhale mlimi, ngati ine . . . Chirichonse chimene icho chiri, Ambuye, kodi Inu mungakhale ndi chiani ine ndichichite?”

¹⁶⁴ Kodi sindicho chimene Saulo anachifuula kumusi kuja, “Ambuye, Inu mungakhale ndi chiani kwa ine kuti ndichite?” Iye anali kumeneka pa chi- . . . pa ulendo wake kumeneka ku—kuti akawuika mpingo wonse mu ndende. Koma ndiye iye anafuula, “Inu mungakhale ndi chiani kwa ine kuti ndichite?” Pamene Kuwala kunayatsidwa, pamene Lawi Lamoto lalikulu linapachikika pamwamba pa iye. “Kodi Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite?”

¹⁶⁵ Nkuganiza, awo ndi mawu abwino kuti titsekerepo, ndi kuti, “Ambuye, Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite? Pamene ine ndikuwona Lemba ili mwangwiro kwambiri likuwululidwa pakali pano; Ambuye, kodi Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite?”

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

¹⁶⁶ Ine ndikupempha aliyense muno kuti mufufuze mitima yanu tsopano ndi kumafunsa funso limenelo, “Ambuye, Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite?” Ndipo inu anthu, ngati inu mukadali pa mawaya a lamya uko kudutsa fuko lonse ili, inu muweramitse mutu wanu ndi kumufunsa, “Ambuye, Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite? Powona kuti ife tiri pano mu masiku otsiriza ndi maora otsiriza, ali mwangwiro chotero basi patsogolo pathu, akuwululidwa momveka kwambiri, Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite?”

¹⁶⁷ Wokonedwa Mulungu, pamene iwo akukufunsani Inu funso limenelo; ine ndikudzifunsa, ndekha, kwa Inu, kodi Inu mungakhake ndi chiani kuti ine ndichite, Ambuye, pamene ine ndikuzindikira kuti tsiku lirilonse liyenera kuwerengedwera. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine, Ambuye, kuti ndikhale moyo chotero kuti tsiku lirilonse, ilo lidzawerengedwera kwa ulemu Wanu ndi ulemerero.

Ine ndikupemphera kuti Inu mumuthandize aliyense konse kudutsa fukoli, ndi iwo pano amene alipo mu kachisi pamene ife tiri kufufuza mitima yathu ndi kuti, “Ambuye, Inu mungakhale ndi chiani kuti ine ndichite? Nchiani ine ndingakhoze kuchita, Ambuye, kuti ndipitirize Ufumu Wanu ndi Cholinga Chanu?” Perekani izi, Mulungu.

Tifufuzeni ife, mitima yathu, ndipo tiyeseni ife. Ngati pakhala pali kusaweruzika kulikonse mwa ife, Ambuye, umbombo uliwonse, zolinga zoyipa zirizonse kapena zofuna, O Mulungu, tiyeretseni ife ndi Magazi a Mwana Wanu, Yesu Khristu, yemwe ife modzichepetsa tikuvomereza chitetezero Chake cha imfa Yake ndi chiwukitsiro Chake. Ndi kukhala olungamitsidwa pa kukhulupirira kuti Iye anachita izi, ife mokondwera tikuvomereza dongosolo la chipulumutso limene Inu munatipatsa ife, kwa ife.

Atate, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Uthenga wa tsikuli, chimene ife tikukhulupirira ndi kwa chimene ife tiri kugwiritsako, kuti tizidziwa ndi kukhulupirira kuti iwo ndi Mawu Anu ndi Uthenga Wanu. Osati kuti tikhale osiyana ndi anu ena, koma kuti tiyesere kuti tikhale mochuluka monga Yesu Khristu Yemwe ali chitsanzo chatu.

¹⁶⁸ Wokonedwa Mulungu, itaikidwa pano ndi mipango, ndipo pali anthu odwala paliponse. Ndi ine mwiniwanga, Ambuye, ine ndatopa ndi wofooka, mmawa uno. Ine ndikupemphera kuti Inu mutithandize ife, wokonedwa Mulungu. Ife tiri kuyang’ana kwa Inu pofuna mphamvu. Inu ndinu Mphamvu zathu. Inu mwathandizapo ochuluka kwambiri, wokonedwa Mulungu.

¹⁶⁹ Tsiku lina, ndiri kuganiza kumusi uko mu nkhalango, ndikuyenda mozungulira ndi M’bale Banks Woods, pamene madokotala. . . Mtima wake unali moyipa kwambiri iye samakhoza nkomwe kuyenda pozungulira. Ndiye kuganiza momwe ine. . . ndimadziwira mochepa pamwamba apo, poyenda mu mapiri amenewo atachitika masomphenya aja, “Ine ndiyenera kuwupeza mkango umenewo. Ine ndiyenera kuwuona mkango umenewo utaphedwa.”

Ndiyeno ndikubwera pansu uko, ndipo nditaima uko ku Tucson, ku Cafeteria ya a Furr, ndi kuwona zovala zake zonse zitakhuchumukira pansu, maso ake atalenguka. Ndinati, “Mulungu, ngati Inu mungakhoze kundisonyeza masomphenya,

a komwe mkango uli, ndithudi Inu mukhoza kundisonyeza za M'bale Woods.”

Ndiyeno iwo anabwera, “Kaike manja ako pa iye.”

Ndipo pano iye ali lero, kumbuyo, M'bale wathu Banks kachiwiri, wamphamvu, akuthamanga kukwera-ndi-kutsika mapiri amenewo. Momwe ife tikukuthokozerani Inu, Mulungu wokonedwa. Inu muli Mulungu yemweyo kwa tonse ife monga Inu mungakhale kwa M'bale Woods. Ine ndikudziwa Inu mumamukonda iye, chifukwa iye ndi wantchito Wanu, woonamtima ndi wodzipereka.

¹⁷⁰ Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu wokonedwa, kuti Inu muchite naye mmodzi aliyense wa ife, ndipo mutikhululukire ife machimo athu, ndipo muchize matenda athu pa matupi athu. Tipangeni ife mochuluka monga Inu, tsiku ndi tsiku, Ambuye, mpaka ife titadza mu thunthu lonse ilo la Yesu Khristu. Perekani izi, Ambuye. Ine ndikudalira kuti Inu mwafufuza mtima uliwonse, tsopano, ndipo ife tidziwa choti tichite. Ife tikupempha kuti Inu mutidalitse ife tsopano, mu Dzina la Yesu.

¹⁷¹ Ndipo pamene ife tiri nayo mitu yathu itaweramitsidwa, kodi alipo aliyense pano, kapena kunjwa mu—mu dziko la lamyakudutsa fukoli, amene mukangofuna basi kuti, pamene inu mukupemphera, ndipo mutu wanu utaweramitsidwa, ingokwezani mmwamba dzanja lanu kwa Mulungu tsopano. Ndi zonse zimene inu mungakhoze kuchita; iwo achulukanamo muno mmawa uno. Ingokwezani dzanja lanu kwa Mulungu, ndi kuti, “Mulungu, ndipangeni ine mochuluka ngati Yesu. Ine—ine ndikufuna kukhala mochuluka monga Yesu.” Mulungu akudalitseni inu. Kunja mu dziko kudutsa fukoli, manja angokhala paliponse, kungokhala khamu lamphamvu. Ndiponso, langa lakwezedwa. “Ine ndikufuna kuti ndikhale mochuluka monga Iye. Ndifufuzeni ine, Ambuye, ndipo mupeze ngati pangakhale choyipa chirichonse mwa ine; chitengereni icho kunjwa. Ine—ine ndikufuna...” Chiyani? Ife tangokhala pano motalika chotere, komabe ife tichoka kaya ndinu... kaya, ziribe kanthu chimene inu muli, ndinu wolemera bwanji, ndinu wosauka bwanji, wamng'ono bwanji, wamkulu bwanji.

¹⁷² Nditaima dzulo kwa—laling'ono, gulu losawuka la anthu komwe uko mu phiri, kumusi ku... pa mtsinje. Kunali banja laling'ono uko, bambo yemwe ine ndakhala ndikuyankhula naye za Mulungu, motalika kwambiri. Anabwera uko, mkazi wake wamng'ono, ana asanu ndi awiri kapena asanu ndi atatu; iye, kanthu kakang'ono kwambiri, kowonda, kunjwa uko akuyesera kugwira ntchito, madola angapo pa tsiku. Ndipo mwamunayo amamulola iye kuti azikhala moyo mu nyumba yaying'ono yokalamba. Ndipo uko mkazi wake kumtunda uko, pafupi atakonzeka kuti akhale ndi mwana wina, ndipo iye anali ndi nkhwangwa yotambalala yaikulu pamwamba

apo, yowazira nkhuni, kuti ayisololere iyo pansu; mwana ali pa phewa limodzi, akusolola nkhuni ndi linalo; anatsika kuti adzadule nkhuni zimenezo, kuti ayike mchitini nthuza zakuda zina, kuwopa kukhala ndi njala kupyola mu chirimwe. Mai, momwe ife tinamumvera chisoni iye! M'bale Woods ndi ine tinapita ndipo tinakatenga galimoto, ndipo tinapita kumeneko ndipo tinakamudulira iye nkhuni, ndi kuzibweretsa izo umo. Iye, mkazi wamng'ono woyamikira, atangoima pamenepo. Ine ndinamumvera chisoni iye. Ndipo ife tinakhala tikuwapempherera iwo.

¹⁷³ Ndipo mwana wake wamng'ono anatenga khunyu. Ife tinapita ndi kukamupempherera mwana wamng'onoyo, ndipo Mulungu anamuchiritsa iye. Ndipo tsiku lina, mwamuna wake anali ndi thumbo, ndipo tinalowa umo . . .

Ine ndinakhala ndikuyankhula kwa iye. Iye ankasuta, onse a iwo. Mkaziyo ankagwiritsa ntchito fodya, ndipo mwamunayo ankatero, nayenso, chenicheni cha anthu aku phiri. Ndiyeno ine ndinakhala ndikuyankhula ndi iwo za izo. Ndipo dzulo mmawa pamene ine ndinalalowa umo, pafupi ndi kuwala kwa tsiku, apa iye anabwera akutuluka, atagwira manja ake limodzi, ndipo anati, "M'bale Billy, ndine munthu wosinthika." Iye anati, "Ine ndasuta ndudu yanga yotsiriza, ndipo ine ndiri ku mbali ya Ambuye."

Mkaziyo anati, "Ine ndangosuta ndudu yanga imodzi yotsiriza, inenso."

O, bzalani mbewu! "Ine Ambuye ndaitsirira. Ine ndiziitsirira iyo usana ndi usiku, kuwopa ena angadzaikhwathule iyo kuchokera mmanja Anga."

¹⁷⁴ O Mulungu, ndichitireni chifundo tsopano, ine ndikupemphera, ndipo tipatseni ife zokhumba za mtima wathu, chifukwa mu mitima yathu ife tikufuna kuti tizikutumikirani Inu. Tsopano, Atate, iwo onse ali mmanja Mwanu, paliponse. Iwo ndi ana Anu. Muchite nawo iwo molingana ndi chifundo, Ambuye; osati mu chiweruzo, koma mu chifundo. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁷⁵ Inu mukumukonda Iye? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mtima wanu wonse! Tsopano, inu amene muli ndi mipango, mukhoza kuitenga iyo.

Ndipo tsopano, misonkhano yathu, ine ndikuganiza iyo iyamba molawirira pang'ono, seveni koloko, kapena chinachake chonga icho. M'bale Neville alengeza izo, mu miniti chabe, za pamene titayambire.

Kodi pali ubatizo, ine ndikulingalira, mmawa uno? [M'bale Neville ati, "Madzi ali okonzeka."—Mkonzi.] Madzi ali okonzeka, ngati munthu wina ali pano ndipo sanabatizidwe panobe mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, bwanji, izo ndithudi ziri . . . Madzi ali okonzekera ku utumiki wa ubatizo.

¹⁷⁶ Ife tikuyamukira abale onse otumikira. Ine ndikumuwona M’bale. . . Kodi msonkhano wanu unali bwanji, unayenda bwino bwino, M’bale Parnell? Ndi M’bale Martin, ndi, o, ochuluka kwambiri a iwo pano, M’bale Lee Vayle. O, pangokhala atumiki paliponse pa malo. Ife ndithudi tikuyamikira inu kukhala muli pano, kudzayanjana ndi ife pozungulira Mawu.

¹⁷⁷ Mwina inu simungakhoze kuvomerezana ndi ine ndendende basi pa Ichi; sindiri kukufunsani inu kuteru, inu mukuona. Chinthu chokha, inu mungolingalira Izo. Chimene inu mundiuza ine, ine ndimachilingalira icho. Ngati atumiki angakatenge tepi, ndipo iwo nkuti, “Chabwino, ine ndikutsutsana nazo.” Izo ziri bwino, m’bale wanga. Inu mukhoza kukhala m’busa wa nkhosa zina; inu—inu muziwadyetsa iwo chirichonse chimene inu mukukhumba kuteru.

Ine ndikuyesera mwakukhoza kwanga kuti ndingokhala basi ndi Mawu, kwa awa amene aikidwa mmanja mwanga kwa Mulungu, chifukwa nkhosa zimafuna chakudya cha nkhosa, ndithudi. “Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa.” Ndipo ndi chimene ife timakhala nacho moyo, Mawu aliwonse amene atuluka. . . Osati onse. . . Osati kokha Mawu pano ndi apo; koma Mawu alionse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu, ndicho chimene oyera ayenera kukhalira moyo nacho.


Tiyeni ife tiyime tsopano ku mapazi athu. Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu. . .

Ndipo M’bale Neville, inu muli ndi chinachake chimene inu mukufuna kuti munene kwa iwo? [M’bale Neville akuti, “Ayi.”—Mkonzi.] M’bale Mann? Chabwino.

Aliyense akumverera bwino? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino.

Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu.

Ine ndikuti ndimufunse M’bale Lee Vayle ngati iye angabwere kuno, kapena iye angakhoze. Ngati inu mungakafike apo, M’bale Vayle, ngati inu mungakhoze.

M’bale Vayle ndi m’bale wathu pano, mlembi wa mabuku. Ndipo iye akukonzeketsa bukhu tsopano, *Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo*, ndipo akugwira ntchito pa *Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri*. Ndipo ife posachedwapa tikuyembekeza kuti tikhala nawo iwo atatuluka posachedwapa kwambiri. Chabwino. M’bale Lee Vayle, Mulungu akudalitseni inu. 

KHRISTU AKUWULULIDWA MU MAWU AKE OMWE CHA65-0822M
(Christ Is Revealed In His Own Word)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikiidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Ogasiti 22, 1965, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 2000 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2000 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org